# KULONGOSOLA MAHADITH 40 A MNENERI (SAW) KWA ACHINYAMATA

كتاب الأربعين الولدانية

**WOMASULIRA M'CHICHEWA NDI:**
**Sheikh Abdul-Rahman Kalako**

**WOGAWA MWAULERE NDI:**
**AFRICA MUSLIM AGENCY**

**Mawu Oyamba**

**Kuyamikidwa konse ndi kwa Allah Mbuye wa zolengedwa zonse. Madalitso ndi mtendere zikhale pa Mneneri wathu Muhammad, a ku banja kwake, ndi mas'haba (ophunzira) ake onse. Pambuyo pa mau awa:**

مُقدِّمةُ الكتاب

الحمدُ لله ربِّ العالمين، والصلاة والسلام على نبيِّنا محمَّدٍ، وعلى آله وصحبه أجمعين، أمَّا بعد:

**Ndithu ma Ulama adalemba mabuku ambiri okhudzana ndi "Mahadith 40". Otchuka kwambiri mwa iwo ndi: "Al Ar'baiina Al-nawawiyyah". Ili ndi buku la mahadith makumi anayi kuchokera m'mahadith a Mneneri (SAW) omwe adawasonkhanitsa ndi Imaam Al-nawawiy kuti ophunzira aloweze pa mtima ndi kutinso adziwe matanthauzo ake.**

فقد ألَّف العلماء كُتُباً كثيرةً في «الأربعين»، أشهرها: «الأربعون النوويَّة»، وهي أربعون حديثاً من أحاديث النبي ﷺ جَمَعَها الإمام النووي ليحفظها طلبة العِلْم وليتفقّهوا في معانيها.

**Ndipo mwa mabuku ena momwe alemba mahadith makumi anai ndi buku (lotchedwa) 'Al ar'baiina fii dalail al-tauhiid " lolembedwa ndi Al Harawiyy, komanso buku la 'Al ar'baiina Al- ilahiyyah la Ibn Al-Mufadhal ndi buku (lotchedwa) 'Al ar'baiina Al- bul'daniyyah la Ibn Asaakir, ndi enanso ambiri.**

ومن الكُتُب التي جَمَعَتْ أربعين حديثا: كتاب «الأربعين في دلائل التوحيد» للهروي، وكتاب «الأربعين الإلهيَّة»، لابن المُفَضّل، وكتاب «الأربعين البلْدانيَّة» لابن عساكر، وغيرها كثير.

**Ndithu Allah wapamwamba wandilemekeza kotero ndasonkhanitsa mahadith 40 mwa Mahadith afupiafupi pa mitu yosiyanasiyana ya**

وقد أكرمني الله تعالى فجمعتُ أربعين حديثاً من الأحاديث القِصار، في موضوعاتٍ شرعيَّة متنوِّعة؛ وذلك

**malamulo a Chisilamu kuti ana athu (amuna ndi akazi) aloweze pa mtima ndi kumvetsa matanthauzo ake. Ndipo ndalitcha bukuli "Al ar'baiina Al- Wil'daniyyah" ndipo Mahadith onse ndi (a sahih) woona omwe adawatulutsa ma Imaam awiri olemekezeka ndipo adagwirizana - Al- Bukhariy ndi Muslim, kapena ndi Mahadith omwe mmodzi mwa awiriwa adawasonkhanitsa, chifundo cha Allah chikhale pa iwo awiriwa.**

**لكي يحفظَها أولادُنا (ذكوراً وإناثاً) وليتفقَّهوا فيها، وسمَّيتُها «الأربعين الوِلْدانيّة»، وكلُّها من الأحاديث الصحيحة التي اتَّفق على إخراجها الإمامان الكريمان البخاري ومسلم، أو من الأحاديث التي أخرجها أحدهما، رحمة الله عليهما.**

**Ndipo ndalongosola hadith iliyonse m'mahadith a "Al Ar'baiina Al-Wil'daniyyah" kulongosola pofotokozera cholinga chake mwachidule uku ndikuonetsetsa kuchita chidule poterepo koma momveka bwino mmene ndingathere.**

**وقد شرحتُ كُلَّ حديثٍ من أحاديث «الأربعين الوِلْدانيّة» شَرْحاً يُبَيِّن المُرادَ منها إجمالاً، مُراعياً في ذلك الاختصار والوضوح قدْرَ الإمكان.**

**Ndipo ndili ndi chiyembekezo chachikulu komanso chilakolako chochuluka kuti Allah Wapamwambamwamba ailandira bwino ntchitoyi komanso kuti pambuyo pake ichitikanso mwayi ndi kulandiridwa ndi anthu ndi kuicheukira poloweza pa mtima, kuphunzitsana, kuiwerenga payekhapayekha, m'magulu, kuchititsa mipikisano ndi maphunziro apadera m'misikiti, m'masukulu, m'makalabu ndi m'nyumba.**

**وَلِي أملٌ عظيم، ورجاءٌ كبير، في أن يتقبّلها الله تبارك وتعالى بقبولٍ حَسَن، وأن تَحْظى –بعد ذلك– بقبول الناس وإقبالهم: بالحِفْظ والمُدَارسة، وبالقراءة الشخصيَّة والجماعيَّة، وبإقامة المُسابقات والدورات في المساجد والمدارس والنوادي والبيوت.**

**O! Allah tipatseni maphunziro aphindu, ntchito yolungama ndi kuthekera pa zinthu kopitirira.**

**O Allah! Perekani madalitso ndi mtendere pa Mneneri wathu Muhammad.**

**Muhmmad bin Sulaiman bin Abdullah Almohanna**
**Riyadh**
**00966505490525**
**Twitter: @almohannam**
**Email: almohanna.m@gmail.com**

**اللهمَّ ارزقنا العِلْم النافع، والعمل الصالح، والتوفيق الدائم.**

**اللهمَّ صلِّ الله وسلِّمْ وباركْ على نبيِّنا محمَّد.**

**محمَّد بن سليمان بن عبد الله المهنا**
**الرياض**
**00966505490525**
**تويتر: @almohannam**
**إيميل: almohanna.m@gmail.com**

## Hadith 1

**Kuchokera kwa Abdullah bin Umar bin Al-khataab (RA) adati: Mtumiki wa Allah (SAW) adati: Chisilamu chamangidwa pa (zipilala) zisanu: Kuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah yekha ndipo ndithu Muhammad ndi Mthenga wa Allah, kupemphera (Swalaat), kupereka Zakaat, (kuchita mapemphero a) Hajj ndi kusala m'mwezi (onse) wa Ramadhan". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديثُ الأوَّل

عَنْ عَبْدِ اللهِ بْنِ عُمَرَ بْن الخَطَّابِ رَضِيَ اللهُ عَنْهُمَا قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللهِ صلى الله عليه وسلم بُنِيَ الإِسْلاَمُ عَلَى خَمْسٍ شَهَادَةِ أَنْ لاَ إِلَهَ إِلاَّ اللَّهُ ، وَأَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولُ اللهِ ، وَإِقَامِ الصَّلاَةِ ، وَإِيتَاءِ الزَّكَاةِ وَالْحَجِّ ، وَصَوْمِ رَمَضَانَ. متفق عليه.

***Kulongosola***

***Mu hadithyi Mneneri wathu SAW akutifotokozera momveka bwino kuti ndithu pali zinthu zisanu zomwe ndi zofunikira kwambiri komanso zokakamizidwa koposa m'chipembedzo cha Chisilamu. Ndiye zinthu zimenezi zimatchedwa (Arkaanul – Islam) zipilala za Chisilamu.***

***Chipilala choyamba: Kuikira umboni kuti palibe wina wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah ndipo ndithu Muhammad ndi mthenga wa Allah. Chipilala chimenechi ndi chachikulu kwambiri mwa zonse. Ndipo amene angayankhule pa lilime lake kuti: ' Ash hadu an laailaha illa llah wa anna Muhammadan rasuulu -llaah' nakhulupirira mu mtima mwake ndithu iyeyo walowa Chisilamu.***

***Chipilala chachiwiri: Kupemphera Swalaat mwadongosolo. Ndithu Swalaat ndi nsichi yaikulu kwambiri pambuyo pa shahaada ziwirizi kotero***

***Mneneri SAW adaitchula Swalaat pambuyo pa shahaada ziwiri mondondozana.***

***Chipilala chachitatu: Kupereka Zakaat. Zakaat ndi chuma choperekedwa chomwe chili ndi mulingo oikidwa pa shariya. Msilamu amakakamizidwa kuchipereka kwa wosowa, wosauka ndi ena oyenera.***

*Chipilala chachinai: Kusala m'mwezi wa Ramadhan. Zili waajib (zokakamiza) kwa Msilamu kusala m'mwezi wonse wa Ramadhan kupatula okhawo omwe ali ndi chowiringula (chovomerezeka).*
*Chipilala chachisanu: (Kuchita mapemphero a) Hajj ku nyumba yolemekezeka ya Allah. Kutero ndi waajib kwa amene angakhale ndikuthekera kopitako kumeneko kamodzi pa umoyo wake onse.*
*zi ndiye zipilala zomwe zamangika pa izo chipembedzo cha Chisilamu. Ndipo tsatanetsatane wa malmulo ake komanso miyambo yake zalongosoledwa m'mabuku a aqeeda ndi fiqh.*

## Hadith 2

**Kuchokera kwa Anas bin Malik (RA) adati: Mneneri SAW adafunsidwa za machimo akuluakulu. Iye adati: "Kuphatikiza Allah ndi chinthu china popembedzedwa, kunyoza makolo awiri, kupha munthu (wosachimwa) ndi kupereka umboni wabodza". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثاني

عَنْ أَنَسٍ رَضِيَ اللهُ عَنْهُ قَالَ سُئِلَ النَّبِيُّ
صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ عَنِ الْكَبَائِرِ قَالَ
الْإِشْرَاكُ بِاللهِ وَعُقُوقُ الْوَالِدَيْنِ وَقَتْلُ النَّفْسِ
وَشَهَادَةُ الزُّورِ». متفق عليه.

*Kulongosola:*
*Mu Hadith yatsogola ija Mneneri SAW anatitchulira zinthu zisanu zomwe ndi zofunikira koposa komanso zokakamizidwa kwambiri mu chipembedzo cha Chisilamu. Zinthu zimenezi zimatchedwa zipalala za Chisilamu.*
*Tsono mu hadith iyi Mneneri SAW akutiuza za zinthu zinai zomwe ndi machimo akuluakulu.*
*Tsono machimo akuluakulu: Amenewa ndi machimo akuluakulu chifukwa choti machimo sali pa mlingo umodzi koma kuti adagawidwa mu zigawo ziwiri zomwe ndi: Akuluakulu ndi ang'onoang'ono.*
*Ndipo machimo akuluakulu omwe Mneneri SAW wanena mu hadith yi ndi anai: Loyamba: Kuphatikiza Allah ndi chinthu china. Ndithu kutero kumam'tulutsa Msilamu m'Chisilamu ndipo kumamulowetsa mu ukafiri komanso kumam'chititsa kukakhala ku ng'anjo ya moto kwamuyaya. Monga mmene Allah akunenera kuti:*

*“ Ndithudi amene angamphatikize Allah ndi chinthu china ndithudi Allah waletsa kwa iye kukalowa ku munda wamtendere ndipo malo ake ndi ku moto ndipo anthu ochita zoipa sadzakhala ndi athandizi. “ Al-maidah 72. Ndipo ma ayat komanso mahadith onyozetsa shirk ndi kuchenjezo ku mchitidwe umenewo komanso kufotokozera mavuto ake ndi ambirimbiri. Ndithu shirk ndi tchimo lalikulu koposa lomwe Allah wachimwidwira nalo.*

*Lachiwiri: Kunyoza makolo. Zitsanzo zina za kunyoza makolo ndi kusathandiza, kusayendera, kuwasautsa ndi mau kapena zochita, kusawamvera, ndi kuwachitira nkhanza za mitundu yosiyanasiyana. Monga mmene kulili kunyoza makolo awiri ndi chinthu chonyansa komanso choletsedwa, ndiye ndithu kuwachitira zabwino makolo awiri ndi chinthu choyamikika koposa kwa Allah. Kuterokonso ndi chifukwa chopezera chiyanjo cha Allah komanso chikondi Chake komanso ndi njira yopezera chikhululuko Chake komanso kukalowa ku Jannat Yake.*

*Lachitatu: Kupha munthu wosalakwa. Kupha ndi tchimo lalikulu ndipo limadzetsa mkwiyo wa Allah, komanso ndi chifukwa cholowera ku moto. Monga momwe Allah akunenera kuti: “ Ndipo amene angaphe Msilamu mwadala, mphoto yake ndi jahannama, mmenemo adzakhala nthawi yaitali. Ndipo Allah amkwiira ndi kumtemberera ndi kum’konzera chilango chachikulu”. An-nisa’ 93.*

*Lachinai: Kupereka umboni wabodza. Amene angapereke umboni wabodza pa (nkhani ya) mnzake ndithu wabweretsa mau oipa ndinso ndi tchimo mwa machimo akuluakulu. Ndi waajib kwa Msilamu kukhala wonena zoona pa chilichonse mwa zina popereka umboni. Choncho ngati wapemphedwa kuikira umboni pa kanthu kenakalikonse chimodzimodzi ndi ku mabwalo la milandu kapena kulikonse atero mwachilungamo ndi moona mtima ndipo apewe bodza kuti asagwere mu tchimo m’machimo akuluakulu.*

## Hadith 3

**Kuchokera kwa Abdullah bin Amru (RA) adati: Mtumiki wa Allah (SAW) adati: “Msilamu (weniweni) ndi amene lilime lake ndinso manja ake, Asilamu (anzake) ali otetezeka.” Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثالث

عَنْ عَبْدَ اللَّهِ بْنَ عَمْرٍو، قَالَ: قَالَ رَسُولُ اللهِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ: « الْمُسْلِمُ مَنْ سَلِمَ الْمُسْلِمُونَ مِنْ لِسَانِهِ وَيَدِهِ ». متفق عليه

***Kulongosola:***

***Msilamu angathe kukhala wamphavu pa Chisilamu kapena wofooka. Chimodzimodzi wokhulupirira angakhale wolimba pa chikhlupiriro kapena wofooka. Msilamu amene amene angakhale ndi mbiri ya kulimba kwa Chisilamu chake komanso ndi kukwanirira kwake, ameneyo ndi amene ali Msilamu woonadi ndipo Chisilamu chake ndi choonadi chomwe Allah amachikonda ndi kusangalala nacho. Ndithu atiuza Mneneri (SAW) mu hadith yi kuti Msilamu wachoonadi ndi yemwe amasunga lilime lake ndi dzanja lake. Tero sasautsa Asilamu kudzera ku lilime ngakhale dzanja lake. Samawatukwana, samawajeda, samawazunza ndi lirime lake komanso samawamenya komanso sawachitira choipa chilichonse angakhale kuwachitira mtopola ndi dzanja lake. Mbiri izi ndi za amene Chisilamu chake chakwanirira kotero Asilamu ali otetezeka ku lirime lake komanso dzanja lake. Komano yemwe avutitse Asilamu kudzera ku lilime ndi dzanja lake, Chisilamu chake ndi chopunguka ndipo chikhulupiriro chake ndi chofooka ndipo sali wokondedwa ndi Allah Wotukuka Wapamwamba.***

## Hadith 4

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mneneri SAW adati: “Zitatu ndi zizindikiro za wachinyengo: Akayankhula amanama, akalonjeza amaphwanya (lonjezo) ndipo akasungitsidwa (katundu) sakhulupirika”. Al-Bukhariy ndi Muslim.**

**الحديث الرابع**

**عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ ، عَنِ النَّبِيِّ صلى الله عليه وسلم قَالَ: « آيَةُ الْمُنَافِقِ ثَلاَثٌ إِذَا حَدَّثَ كَذَبَ ، وَإِذَا وَعَدَ أَخْلَفَ ، وَإِذَا اؤْتُمِنَ خَانَ. ».** متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Achinyengo ndi zolengedwa zoipa mwa zolengedwa za Allah ndipo ndithu Allah watiuza za iwo pa (zomwe wakonzera) tsiku lotsiriza. Ndipo Iye adati “ Ndithu achiphamaso (achinyengo) adzakhala pansi penipeni pa moto “ An-Nisa’ 145.***

*Mu hadith yi watiuza Mneneri SAW zizindikiro zitatu za achinyengo kuti titalikirane nazo ndinso tichenjere ndi izo.*
*Chizindikiro choyamba: Bodza*
*Chizindikiro chachiwiri: Kuphwanya pangano.*
*Chizindikiro chachitatu: Kusakhulupirika.*

*Zizindikiro zitatu izi ndi mbiri za wachinyengo. Tsono wokhulupirira ndithudi akayankhula, amayankhula zoona ndipo sanama, akamulonjeza wina wake chithu samaswa lonjezolo, wina wake akasungitsa katundu kwa iye, ndithudi amabweza kwa iye mofulumira pa nthawiyake mosachedwetsa ndinso mosazengereza. Chimodzimodzinso winawake akamuuza nkhani kapena chinsinsi namupempha kubisa nkhaniyo kapena chinsinsicho ndithu iye amakwaniritsa ndipo saulula kwa wina chifukwa kufalitsa chinsinsi ndi mbali imodzi ya chinyengo. Timpemphe Allah atitalikitse ndi zimenezi.*

## Hadith 5

**Kuchokera kwa Jabir bin Abdullah (RA) adati: Mtumiki wa Allah (SAW) adati: “ (Chosiyanitsa) Pakati pa munthu ndi uchikunja ndinso kusakhulupirira ndiko kusiya kupemphera Swalaat “. Muslim.**

الحديث الخامس

عَنْ جَابِرِ بْنِ عَبْدِ اللهِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا ، قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صلى الله عليه وسلم: « بَيْنَ الرَّجُلِ ، وَالْكُفْرِ تَرْكُ الصَّلاةِ ». رواه مسلم.

*Kulongosola:*
*Swalaat ndi chipilala chachikulu pambuyo pa shahadat ziwiri ( Shahaadat an lailaha illa Llah wa shahadat anna Muhammadan rasoollah -Kuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah basi ndi kuikira umboni kuti Muhammad ndi mtumiki wa Allah), choncho lidadza lamulo lakupemphera m’ndime zambiri za Quran ndinso m’mahadith ochuluka a Mneneri SAW.*

*Ndiye Hadith imeneyi ikutisonyeza kuopsa kwa kugwera mphwayi nkhani ya kupemphera Swalaat. Ndithu wanenetsa Mneneri SAW mu Hadith imeneyi kuti ndithu palibe china (chosiyanitsa) pakati pa munthu ndi uchikunja ndinso kumuphatika Allah pomupembedza ndi zinthu zina kupatula kusiya kupemphera Swalaat. Ndithu kuisiya Swalaat, ndiye kuti wafika pa ukafir (kusakhulupirira) ndinso pa shirk billah. Tiyeni tizitchinjirize mwa Allah kuthawa zimenezi. M'menenmu muli umboni woonekera kuti ndithu kusiya kupemphera ndi tchimo limodzi m'machimo akuluakulu loononga munthu ndi kumugwetseraku ng'anjo ndipo ndithu likuposa machimo ena akuluakulu monga katapira, chigololo, kuba, kumwa mowa chikhalirecho machimo amenewa ali m'gulu la machimo akuluakulu. Choncho ndi waajib kwa Msilamu aliyense wa mwamuna ndi wamkazi kuchitira khama pa kupemphera Swalaat ndi kujjijirikira mokwanira. Ndipo kutero, kumadzetsa zabwino, madalitso, chakudya ndipo ndi njira yonkera ku Jannat, chikhululukiro ndi chisangalalo cha Allah.*

## Hadith 6

**Kuchokera kwa Abdullah bin Mas'ood (RA) adati: Ndidafunsa Mtumiki wa Allah (SAW) kuti: Ndi ntchito ziti zokondedwa koposa ndi Allah? (Iye SAW) Adayankha: "Kupemphera Swalaat pa nthawi yake (yoikidwa)". Ndipo ndidafunsa: "Kenako"? Adayankha: "Kuchitira makolo awiri zabwino.....mpaka pa mathero a hadith " Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث السادس

**عَنْ عَبْدِ اللهِ بْنَ مَسْعُودٍ، رضي الله عنه قَالَ:
سَأَلْتُ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ:
« أَيُّ الأَعْمَالِ أَحَبُّ إِلَى اللَّهِ ؟ قَالَ:الصَّلاةُ
لِوَقْتِهَا، قُلْتُ: ثُمَّ أَيٌّ؟ قَالَ:بِرُّ الْوَالِدَيْنِ،**

......... إلى آخر الحديث ». متفق عليه.

*Kulongosola:*

*Mas'haba RA nthawi zonse adali kufunsa Mneneri wa Allah SAW ntchito zabwino zomwe Allah amazikonda ndi kuzisangalalira amatero pofuna kuti adziyandikitse nazo kwa Iye (Allah). Ndipo mu hadith yi watiuza*

*sahaba wolemekezeka (Abdullah bin Mas'ood (RA) kuti ndithu iye adafunsa Mneneri wa Allah SAW ntchito zabwino zomwe Allah amazikonda (munthu akachita). Ndipo Mneneri wa Allah SAW adamuyankha natchula kuti ndithu ntchito yofunikira kwambiri kwa Allah komanso yokondeka koposa ndi 'kupemphera Swalaat pa nthawi yake (yoikidwa)'. Apa zikutanthauza nthawi yoyambirira (nthawi ya Swalaat ikakwana). Ndiye kupemphera Swalaat kumayambiriro nthawi itakwana ndi umboni osonyeza kuifunitsitsa ndinso kuikonda (Swalaatiyo). Ndipo yemwe akonde kumvera Allah, Allah am'konda iye. Zofunika kwa Asilamu achimuna ndi achikazi kuchitira khama kwambiri pa Swalaat.amuna apemphere kumayambiriro kwa nthawi m'misikiti pa jamaat (pagulu) ndipo achikazi m'nyumba zao. Ndipo zina mwa zomwe tingakumbutse ndikuti ndithu ndi koyenera kwa Msilamu aliyense adziwe nthawi za Swalaat ndipo kutero ndi chinthu chachikulu. Amene asiye kupemphera Swalaat mwadala mpaka kutha nthawi (ya Swalaatiyo) ndithu wachita tchimo lalikulu mu machimo akuluakulu.*

*Mu Hadith yomweyi kenako Mneneri SAW wanena za ntchito ina ya bwino yomwe Allah amaikonda ndiyo kuchitira zabwino makolo awiri. Ndipo kuchitira makolo awiri zabwino ndi nsembe yaikulu komanso ndi ntchito yosonyeza kumumvera Allah ndinso yokondedwa koposa kwa Iye. Kuchitira za bwino makolo ake awiri ndiko kuti mwana wachimuna komanso wachikazi adziwachitira bwino pa kayankhulidwe kake kmanso m'kachitidwe powamvera, kuwalemekeza, kuwasamalira, osapereka masautso kwa iwo mmau ngakhalenso mu zochita chifukwa kutero ndi kunyonza makolo ndipo ndi tchimo mwa machimo akuluakulu. Tim'pemphe Allah chikhululuko ndi umoyo wathanzi.*

## Hadith 7

**Kuchokera kwa Uthman bin Affan (RA) adati: Mtumiki wa Allah (SAW) adati: Amene achite wudhu (mwandondomeko), nalondoloza wudhuwo kenako napita ku (msikiti kokapemphera) mapemphero okakamiza, napemphera pa jamaat (pa gulu), Allah amam'khululukira iye machimo ake". Muslim.**

الحديث السابع

عَنْ عُثْمَانَ بْنِ عَفَّانَ رضي الله عنه،قَالَ :
قَالَ رَسُولُ اللهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ: «
مَنْ تَوَضَّأَ لِلصَّلاَةِ فَأَسْبَغَ الْوُضُوءَ ، ثُمَّ مَشَى
إِلَى الصَّلاَةِ الْمَكْتُوبَةِ فَصَلاَّهَا مَعَ الْجَمَاعَةِ
غَفَرَ اللَّهُ لَهُ ذُنُوبَهُ.». رواه مسلم.

***Kulongosola:***
***Mu hadith yi Mneneri SAW watiuza za ntchito yaikulu yomwe munthu akaigwira, Allah amamulemekeza pomupatsa malipiro okwanira ndipo malipiro amenewa ndiko kum'khululukira machimo ake. Ntchito imeneyi imakhudzana ndi Swalaat ndipo ili ndi zinthu zitatu zomwe Msilamu amachita pofuna kudziyandikitsa kwa Allah Wamphamvu, Wolemekezeka:***
***Ntchito yoyamba: Kuchita Wudhu molondoloza. Kulondoloza ndiko kufikitsa madzi pa ziwalo zonse zoyenera pa Wudhu mokwanira ndithu posasiya mkute.***
***Ntchito yachiwiri: Kupita ku msikiti kokapemphera Swalaat zokakamiza.***
***Ntchito yachitatu: Kupemphera Swalaat pa gulu ndi Asilamu anzako. Amene wachita zimenizi moti wachita wudhu molondoloza, napita ku msikiti kenako ndi kupemphera nawo pa gulu ndithu apeza malipiro abwino amenewa, omwe ndi akuti Allah amukhululukira machimo ake. Ndipo dziwani kuti yemwe Allaah wamukhululukira machimo ake ndiye kuti ndi wopambana pa dziko pano ndi tsiku lotsiriza.***

## Hadith 8

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Amene andinamizire mwadala (kuti ndidanena chakuti pomwe sindidanenepo), choncho adzikonzekeretse zotenga malo ake (okhalamo) ku moto". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

**الحدث الثامن**

**عَنْ أَبِى هُرَيْرَةَ** رضي الله عنه، **قَالَ: قَالَ رَسُولُ اللَّهِ** صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ **« مَنْ كَذَبَ عَلَيَّ مُتَعَمِّدًا فَلْيَتَبَوَّأْ مَقْعَدَهُ مِنَ النَّارِ »**. متفق عليه.

***Kulongosola:***
***Kupeka bodza pa hadith ya Mneneri SAW ndi tchimo mwa machimo akuluakulu. Ndipo amene wapeka bodza (pa mau a Mtumiki SAW) nanena kuti ndithu awa ndi mau a Mtumiki SAW (pomwe sichoncho),***

*wadzipekera utchimo waukulu. Ndipo yemwe wafalitsa nkhani yabodza yom'pekera Mtumiki wa Allah SAW popanda kufotokozera kuti ndi hadith yabodza ndithu wapyozamalire komanso wapondereza ndinso walakwitsa kwakukulu. Chodandaulitsa chachikulu kwa iye ndiko kufala kwa nkhani zopeka kum'pekera Mneneri wa Allah SAW. Chodandaulitsanso china ndi chakuti ena mwa akufuna kwabwino – ndi cholinga (chao) chabwino – akuthandizira kufalitsa nkhani zopeka, ichi ndi cholakwika chachikulu ndipo n'koyenera kulangizana ndikuchenjezana pakati pathu za zimenezo.*

*Adanena SAW kuti: " Ndithu kundipekera bodza (machimo ake ndi akuluakulu), n'kosafanana ndi kupekera wina bodza posakhala ine, choncho amene wandipekera bodza (kuti ndidanena chakuti pomwe sindidanenepo) mwadala, choncho adzikonzekeretse kutenga malo ake (okhalamo) ku moto. " Al-Bukhariy.*

*Adanenanso Mtumiki wa Allah SAW kuti: " Yemwe afotokoze hadith (nkhani) kuchokera kwa ine uku akudziwa kuti ndi ya bodza choncho ali mmodzi mwa onama. "Tirimidhiy. Chofunikira kwa ife (ndikuyamba kaye) kutsimikiza kuona kwa hadith (nkhani) tisadanene kuti Mneneri wa Allah SAW adanena. Ubwino wa Allah pa ife, ndithu Iye watifewetsera zambiri nthawi ino nkhani yofuna kutsimikiza choonadi cha mahadith kudzera mmabuku ndi pa intaneti yodalirika. Ena mwa mabuku odalirika pa nkhaniyi ndi mabuku a Shaykh Al-Ba'niy (Allah awachitire chisoni) ndi qasam almawsueat "encyclopedia section" (Ad-Durar As-Saniyyah).*

### Hadith 9

**Kuchokera kwa Abdullah bin Mas'ood (RA) adati: Mneneri SAW adati: "Sakalowa ku jannat (ku munda wa mtendere) amene mu mtima mwake muli kudzitukumula kolemera ngati njere ". Muslim.**

الحديث التاسع

**عَنْ عَبْدِ اللَّهِ بْنِ مَسْعُودٍ** رضي الله عنه،**قَالَ النَّبِيُّ** صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ « **قَالَ لا يَدْخُلُ الْجَنَّةَ مَنْ كَانَ فِي قَلْبِهِ مِثْقَالُ ذَرَّةٍ مِنْ كِبْرٍ**».

رواه مسلم

*Kulongosola:*

***Chisilamu ndi chipembedzo chimalimbikitsa khalidwe labwino ndi mbiri yabwino kotero chidalamula (munthu) kulolerana, kudzichepetsa ndi kudekha (mwa zina). Ndipo chidaletsa kudzipopa, kudzitukumula ndi kudzikuza. Mu hadith yi muli chenjezo kuchokera kwa Mneneri SAW kwa iwo odzitukumula omwe amaeputsa anzawo ndi kumadzikuza pa iwo. Choncho anthu odzikuza sakalowa ku jannat (ku munda wa mtendere). Tim'pemphe Allah atipulumutse ndinso kutitalikitsa (ku mchitidwe onga umeneu). Tanthauzo la mau a SAW akuti: " Sakalowa ku jannat (ku munda wa mtendere) yemwe mu mtima mwake muli kudzitukumula ngakhale kochepa kolemera ngati nyerere. "Ndithu kudzikweza ndi chinthu choopsa kwambiri ngakhale kutakhala kochepa ngati kulemera kwa nyerere womwe ndi mulingo wochepetsetsa. Ndithudi Mneneri SAW adatiuza tanthauzo la kudzitukumula nati: "Kudzitukumula ndi kunyalanyaza choonadi ndi kunyoza anthu". Umboni wina woletsa ndinso kunyazitsa kwa kudzitukumula ndi kuyankhula kwa Mneneri SAW kuti: "Amene adzikuze yekha, kapena kudzitama pa kayendedwe kake, ndithu akakumana ndi Allah Iye ali atamukwiyira". Al-Bukhariy. Ndipo pamene tadziwa kuti kudzikuza ndi tchimo ndinso khalidwe lonyansa, zakakamidwa pa ife kuti tikupewe. Tigwire ntchito zabwino zomwe zingatitalikitse ku zimenezo monga kumvera ulangizi, kutsata chilungamo, kukonda osowa, ofooka, osauka, ndi ogwira ntchito ndi ena otero. Komanso monga kuwalezera mtima anthu otero, kwasamalira ndi kudzichepetsa kwa iwowo ndithu kutero ndi zili mu gulu mwa zomwe zimayeretsa mtima, ndi kuuchapa mbiri yodzipopa, kudzikuza ndi kudzitukumula.***

## Hadith 10

**Kuchokera kwa Uthman bin Affan (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: " Wabwino mwa inu ndi amene waphunzira Al-Qur'an ndipo naphunzitsa ena". Al-Bukhariy.**

الحديث العاشر

عَنْ عُثْمَانَ بْنِ عَفَّانَ رضي الله عنه، قَالَ:

قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ « خَيْرُكُمْ

مَنْ تَعَلَّمَ الْقُرْآنَ وَ عَلَّمَهُ. رواه البخاري

*Kulongosola:*

***Hadith yi ikusonyeza kufunikira kophunzira Al-Qur'an Yolemekezeka ndinso kuiphunzitsa kwa ena. Ndiye Mneneri SAW akutiuza kuti ndithu anthu omwe akuphunzira Al Quran komansoomwe akuiphunzitsa iwowo ndiwo ali abwino koposa mwa anthu onse. Pamene ta'bi Abu Abdul-Rahman Al-Sulamiy (otsatira) olemekezeka adafotokoza hadith yi, (Iye ndi amene adailandira kuchokera kwa Uthman bin Affan (RA) adati: "Ndi chifukwa chake ndakhala malo ano". Izi zikutanthauza kuti iye adakhala zaka zambirimbiri kukhumba atapeza zabwino zomwe zanenedwa mu hadith yolemekezekayi. Choncho ndikofunikira kwa Msilamu wachimuna ndi wachikazi kuikira chidwi pa Al-Qur'an poiphunzira komanso kuikhoza bwino kenakono atenge mbali zoiphunzitsa kwa ena. Ndipo zina mwa zinthu zothandiza ndi zabwino ndi kukhala nao m'magulu ophunzira kuloweza pa mtima Al-Qur'an monga m'misikiti, m'ma madrasa mma insitichuti ndi cholinga chofuna kuphunzira, wotero ali ndi ubwino, dangalira ndi chiongoko.***

## Hadith 11

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: " Mau awiri opepuka pa lilime, olemera pa sikelo, okondedwa kwa Al-Rahman (Wachifundo): "Subhan-Allah wabiham'dih subhan-Allahil- Adhim". (Ulemerero ndi wa Allah ndi Wotamandika ndipo ulemerero ndi wa Allah Wamkulu).**

**Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الحادي عشر

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رضي الله عنه،، قَالَ : قَالَ
رَسُولُ اللهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ :«كَلِمَتَانِ
خَفِيفَتَانِ عَلَى اللِّسَانِ ، ثَقِيلَتَانِ فِي الْمِيزَانِ
، حَبِيبَتَانِ إِلَى الرَّحْمَنِ : سُبْحَانَ اللهِ
وَبِحَمْدِهِ ، سُبْحَانَ اللهِ الْعَظِيمِ ». متفق عليه.

*Kulongosola:*

***Mwa ntchito zina zomwe ndi zabwino koposa, zolemekezeka komanso zazikulu malipiro ake ndi: Kumukumbukoira Allah wapamwambamwamba. Ndithudi watiuza Allah mu Buku Lake mu ndime zambiri***

*komanso Mneneri watiuzanso mu Mahadith ochulukakutindithu kukumbukira Allahndi njira yopezera chikhulukuko komanso malipiro aakulu. Monga mmene wanenera Allah kuti: (Ndithu Asilamu achimuna ogonjera Allah mokwanira, ndi Asilamu achikazi ogonjera Allah mokwanira, okhulupirira achimuna ndi okhulupirira achikazi, omvera achimuna ndi omvera achikazi, oona mtima achimuna ndi oona mtima achikazi,opirira achimuna ndi opirira achikazi, odzichepetsa achimuna ndi idzichepetsa achikazi, opereka sadaka achimuna ndi opereka sadaka achikazi, osala achimuna ndi osala achikazi, osunga umaliseche wawo (ku chiwerewere) achimuna ndi osunga maliseche awo achikazi, otamanda Allah kwambiri achimuna ndi otamanda Allah kwambiri achikazi, Allah wakonzera chikhululuko ndi malipiro aakulu) Ahzaab 35.*

*Komanso watikakamiza Mneneri SAW mu mahadith ambiri za kuchulukitsa Al-Zikr (kukumbukira Allah). Ndipo watifotokozera ubwino wake ndi kufunikira kwake, ndipo adatiikira Al-Azkaar (onena) ku mmawa ndi masana, ena pogona ndi podzuka. Ena mwa Al-Azkaar (wa) akupezeka m'mabuku monga Kitaabul-Azkaar ya Al-Nawawiy, Tuh'fatul-Akhyaar ya Ibn Baaz ndi Hisnul-Muslim ya Qah'taniy ndi ena ambiri. Pali Az-kaar ena omwe alibe nthawi yoikidwa choncho zili bwino kwa Msilamu adzinena pa nthawi iliyone mochulukitsa monga Al-Zikr iyi: "Subhan-Allah wal- ham'du lillah wala'ila'ha illah wallah akbar wala'haula wala'quwwata illa billah"*

*Ena mwa (Al-Azkaar) ndi: Mau awiri akulu awa omwe watiuza Mneneri SAW mu Hadith imeneyi kuti: (Mau awiri opepuka pa lilime, olemera pa sikelo -"Subhan-Allah wabiham'dih subhan-Allahil- Adhim"). Ndithu adatiuza SAW kuti: "Mau awiriwa ndi osiyana ndi ena mu zinthu zitatu":*

*1- Ndi mau opepuka pa lilime tero ngopepuka kwa munthu kubwerezabwereza mosavuta.*

*2- Ndi mau olemera pa sikelo ndipo izi zikutanthauza kuti ndithu amene wanena mau amenewa, apeza malipiro ochuluka (ndipo) Allah adzadzitsa zabwino ndi mawu amenewa pa sikelo ya zabwino zake.*

*3- Ndithudi ndi mau okondedwa ndi Al-Rahman (Wachifundo). Zikutanthauza kuti ndithu Allah Wodalitsika Wotukuka amakonda mauwa. Pa chifukwa cha zonsezi, zikufunikira kwa ife tonse kuikira mtima pa mawu awiri akulu amenewa ndi ena onga iwo mu ma Al azkaar opanda nthawi yeniyeni aja. Ndikutinso tidzichirimika potero ndi kumachulukitsa mu nthawi zonse posatengera mmene tilili kuti tipeze malipiroaakulu kuchokera kwa Mbuye Wolemekezeka.*

### Hadith 12

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Lidandilangiza bwenzi langa SAW zinthu zitatu: "Kusala masiku atatu pa mwenzi ulionse, kupemphera marakat awiri a Al-Dhuha (dzuwa likangokwera pang'ono chakummawa) ndi kupemphera Witr ndisanagone".**

**Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثانيَ عشر

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رضي الله عنه، قَالَ « أَوْصَانِي خَلِيلِي صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ بِثَلَاثٍ بِصِيَامِ ثَلَاثَةِ أَيَّامٍ مِنْ كُلِّ شَهْرٍ وَرَكْعَتَيْ الضُّحَى وَأَنْ أُوتِرَ قَبْلَ أَنْ أَنَامَ ». متفق عليه.

*Kulongosola:*

*Abu Hurairah RA sahaba wolemekezeka woyandikira kwa Mtumiki wa Allah SAW akutiuza langizo lomwe adalangizidwa ndi Mneneri SAW kuti: "Lidandilangiza bwenzi langa". Ndipo liu loti "Khaliil" limatanthauza bwenzi ndipo ndilofanana ndi liu loti "Habiib" lomwe limatanthauza wokondedwa choncho liu loti: "Khaliil" limasonyeza chikondi chodzadza kupyola pachikondi.*

*Abu Hurairah RA akuyankhula kuti: "Lidandilangiza bwenzi langa malangizo atatu:*

*Langizo loyamba: Kusala masiku atatu pa mwenzi ulionse. Kusalaku kuli ndi ubwino wochuluka. Ndithu Mneneri SAW adatiuza kuti: "Kusala masiku atatu pa mwenzi*

*ulionse umapeza malipiro ofanana ngati wasala chaka chathunthu". Uwu ndi mtendere wa Allah pa akapolo ake. Kusala kwa masiku atatu pa mwenzi ulionse ndi kwachifuniro (sunnat) choncho nkololedwa kusala masiku otsatana kapena modumphitsa.*

*Langizo lachiwiri: Kupemphera ma rakaat awiri kapena ochulukirapo a Swalaat - Al-Dhuha pomwe dzuka lakwera pang'ono chakummawa. N'kwabwino kwa Msilamu kupemphera marakah awiri kapena anai kapena ochulukirapo nthawi ya Al-Dhuha (dzuwa likangokwera pang'ono chakummawa). Ndithu malipiro akutero ngochuluka komanso ubwino wake mdi waukulu.*

*Langizo lachitatu: Kupemphera Witr. Swalaat - Witr ndi imodzi mwa Swalaat yabwino m'mapemphero a nafl (Sunnat. Swalaatul- Witr imayamba kutha kwa pemphero la Al-Isha mpaka nthawi ya Adhan ya Fajir. Msilamu amapemphera mwaufulu modzipereka kwa Allah monga rakat imodzi, atatu, asanu kapena oposerapo. Chofunikira kuonetsetsa ndi chiwerengero choti mukagawa ndi ziwiri patsale chimodzi ilo ndilo tanthauzo la Witr. Awa ndi malangizo ochokera kwa Mneneri SAW kwa Abi-Hurairah (RA) ndipo ndi malangizo atonsefe ochokera kwa Mtumiki wathu komanso wokondeka wathu Muhammad SAW.*

## Hadith 13

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: " Kapolo amayandikira pafupi ndi Al-Rabb (Mbuye) wake pamene wagwetsa nkhope yake pansi choncho chulukitsani dua (pempho mukagwetsa nkhope zanu pansi) ". Muslim.**

الحديث الثالثَ عشر

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رضي الله عنه، ، قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : « أَقْرَبُ مَا يَكُونُ الْعَبْدُ مِنْ رَبِّهِ وَهُوَ سَاجِدٌ فَأَكْثِرُوا الدُّعَاءَ ». رواه مسلم.

***Kulongosola:***

***Allah Wamphamvu, Wolemekezeka adalamula akapolo ake kudziyandikitsa kwa Iye kudzera m'mapemphero osiyanasiyana. Njira zina mwa zikuluzikulu zodziyandikitsa nazo kwa Allah ndi kupemphera Swalaat faraidh pagulu ndi nawaafil zake ndipo Msilamu akalowa mu Swalaat, amakhala chifupi ndi Allah Wapamwamba. Ngakhale kuti Swalaat yonse imamuyandikitsa kapolo wokhulupirira kwa Allah, koma ndithu kapolo akagwetsa nkhope pansi, pa nthawiyi, amayandikira koposa kwa Iye. Ndithu kapolo amayandikira kwa Allah akagwetsa nkhope pansi uku akum'tamanda ndi kumuyeretsa ndi kumpempha zosowa zake, pa nthawiyi kapolo amakhala woopa, wodzichepetsa ndinso wosowekera. Ndipo pa chifukwa chimenechi ndithu kugwetsa nkhope pansi ndi amodzi mwa malo amyankho ku maduaa momnga mmene adanenera Mneneri SAW kuti: "Tsono pogwetsa nkhope pansi chitirani khama pochita dua choncho ndi zoyembekezeka kuti muyankhidwe". Choncho zili bwino kwa munthu kutalikitsa pa sajida (nkhope ili pansi), kuchulukitsa madua (pempho). Ndithu kugwetsa nkhope pansi komanso kuchita dua ndi njira imodzi mwa njira zikuluzikulu zopezera zabwino ndi chipambano pa dziko lapansi ndi umoyo uli mkudza.***

## Hadith 14

**Kuchokera kwa Tha'bit bin Ad-hha'k (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Kutemberera mu'min (Msilamu wokhulupirira) kuli ngati kumupha". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الرابعَ عشر

عَنْ ثَابِتِ بن الضَّحَّاكِ رضي الله عنه ، قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : « لَعْنُ الْمُؤْمِنِ كَقَتْلِهِ ». متَّفقٌ عليه.

***Kulongosola:***

***Temberero ndi tchimo lalikulu komanso ndi mnyozo waukulu. Ndithu Mneneri wathu SAW adatichenjeza ku temberero komanso anatiletsa m'Mahadith ochuluka monga adanena mu hadith yi:***

***Kulongosola:***

***Temberero ndi tchimo lalikulu komanso ndi mnyozo waukulu. Ndithu Mneneri wathu SAW adatichenjeza ku temberero komanso anatiletsa m'Mahadith ochuluka monga adanena mu hadith yi: "Kutemberera mu'min (wokhulupirira) kuli ngati kumupha (osachimwa)". Ndipo adatinso: " Musatembererane ndi temberero lochokera kwa Allah ngakhalenso mkwiyo Wake (ponena kuti laanatullah alaika kapena ghadhabullah alaika)". Al-trimidh.***

***Ndipo Mneneri SAW adanena monga mmene zadzera mu Sunan - Abi Daud (RA) kuti: "Ndithu munthu akatemberera china chake popanda chilungamo chenicheni ndithudi temberero limabwerera pa iye". Kutanthauza kuti ndithu temberero limabwerera pa wotembererayo.***

***Tabara'niy adalandira (nkhani) kuchokera kwa Salamat bin Al-Ak'waa (RA) adati: "Tinkati tikaona munthu akutemberera m'bale wake ndithu tidali kunena kwa iye kuti walidzera khomo la tchimo mu machimo akuluakulu".***

***Al-Shaykh Ibn Baaz adati: "Kutemberera Msilamu ndi tchimo m'machimo akuluakulu". Zina mwa zinthu zodandaulitsa, ndiko kufala kutembererana pakati pa Asilamu ambiri. Allah atithandize kuti tisagwe m'tchimo limeneli. Choncho ndi waajib kwa ife tonse: Tiyeni tinyansidwe ndi mchitidwewu, tiupewe ndinso tichenjeze ena ku mchitidweu molimba.***

## Hadith 15

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: Allah Wapamwamba adati: " O! Mwana wa Adam pereka (ndipo) upatsidwa (mochuluka)". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الخامسَ عشر

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رضي الله عنه، قَالَ: قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ« قَالَ اللَّهُ تَبَارَكَ وَتَعَالَى يَا ابْنَ آدَمَ أَنْفِقْ أُنْفِقْ عَلَيْكَ » متفق عليه.

*Kulongosola:*

*Zina mwa mbiri zabwino zomwe Allah wachemelera nazo akapolo Ake okhulupirira ndi kupereka pa njira ya Allah. Allah pazimenezi akunena akunena kuti: " Alif-Lam-Mim. Ili ndi buku lopanda chipeneko mkati mwake ndi chiongoko cha anthu oopa Allah omwe amakhulupilira zosaoneka ndi maso (monga munda wa mtendere, moto, angelo, ndi zina zotere zomwe Allah ndi Mtumiki adazifotokoza), amapemphera Swalaat (moyenera) ndiponso amapereka m'zimene tawapatsa" Al-Baqarah 1-3.*

*Ndipo kupereka kuli m'mitundu yosiyanasiyana monga: mwamuna kwa mkazi wake, ana ake, osowa, osauka ndinso kuthandiza pa zabwino monga kugawa ma Qur'an, mabuku ofunikira, kuchiritsa odwala ndi maporojekiti ena otero.*

*Mu Hadith yi muli lonjezo la Allah Wapamwamba kwa yemwe wapereka chuma chake pa njira zabwino kuti Allah adzamupatsa ndi kumuchulukitsira riziq lake kuchokera mu zabwino Zake ndipo adzampatsa china mmalo mwakekuchokera mu zopatsa Zake zochuluka. Monga adanenera Allah Wamphamvu, Wolemekeza pa ndime iyi: "Nena (Iwe Mneneri): "Ndithu, Mbuye wanga amam'chulukitsira riziq (zaulere) amene wam'funa mwa akapolo Ake ndiponso amam'chepetsera (amene wam'funa) ndipo chilichonse chimene mupereka, Iye adzakupatsani china mmalo mwake, Iye Ngwabwino popatsa zaulere kuposa opatsa". Saba 39.*

*Choncho amene wapereka kubanja lake, kapena kwa makolo ake, abale ake, osowa, osauka kapena kupereka pa njira zabwino zosiyanasiyana, Allah adzampatsa malipiro ndipo adzam'chulukitsira riziq (zaulere), pa zimene adapereka. Ndipo uwu ndi ubwino wa Allah, omwe amaupereka kwa amene wam'funa ndipo Allah ndi mwini ubwino waukulu.*

## Hadith 16

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Sikungam'peze Msilamu kutopa (kapena kufooka), kapena matenda, kapena nkhawa, kapena dandaulo, kapena masautso, kapena kupweteka ngakhale minga yomwe ingamulase, pokhapokha Allah amafuta ndi izi machimo ake". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث السادسَ عشر

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رضي الله عنه ، قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : « مَا يُصِيبُ الْمُسْلِمَ مِنْ نَصَبٍ ، وَلا وَصَبٍ ، وَلا هَمٍّ ، وَلا حَزَنٍ ، وَلا أَذًى ، وَلا غَمٍّ ، حَتَّى الشَّوْكَةُ يُشَاكُهَا ، إِلا كَفَّرَ اللَّهُ بِهَا مِنْ خَطَايَاهُ. ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Pa dziko lapansi munthu amakumana ndi masautso osiyanasiyana monga kutopa, mavuto, nkhawa ndi zodandaulitsa zankhaninkhani. Mu Hadith yi Mneneri SAW akutiuza chinthu chachikulu chomwe tiyenera kuchikumbukira pa nyengo zathu zonse kutero ndi chinthu chomwe chimasangalatsa mtima ndi kubweretsa kudekha. Ndipo chinthu sichingampeze Msilamu monga kutopa, matenda, nkhawa, zachisoni, kukhumudwa (ndi masautso), kapena kupweteka ngakhale kulasidwa ndi minga pokhapokha Allah amafufuta ndi zimenezi machimo ake. Kutheka kuti kukumana ndi masautso ndi njira yochotsera machimo ndi kuwafafaniza tero Msilamu amatuluka m'mavuto ali wokhululukidwa, woyera, woyandikira kwa Mbuye wake komanso Mthandizi wake. M'mau ake a Mneneri SAW akuti: "….. Ngakhale kulasidwa ndi minga". Uwu ndi umboni (wokwanira) kuti ndithu masautso amene munthu amam'peza ndi dipo kwa iye, ngakhale masautso ochepa monga kulasidwa ndi minga. Munthu akadziwa izi, asangalale chifukwa cha mtendere wa Allah ndipo ayesetse kukhala wopirira, wachiyembekezo ndi wokhutira ndi Allah. Amene ayamike zomwe Allah wampatsa, Allah adzalandira ntchito zake ndipo adzam'lemekeza, adzam'patsa mtendere ndi zaulere Zake zochuluka.***

## Hadith 17

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati "Simungakalowe ku jannat (ku munda wa mtendere) mpaka mutakhulupirira, ndipo simungakhulupirire mpaka mutakondana, Kodi ndikusonyezeni chinthu ngati mungachite chinthucho mudzakondana? Falitsani salaam pakati panu (mukakumana)". Muslim.**

الحديث السابعَ عشر

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رضي الله عنه قَالَ: قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ « لَا تَدْخُلُونَ الْجَنَّةَ حَتَّى تُؤْمِنُوا وَلَا تُؤْمِنُوا حَتَّى تَحَابُّوا أَلَا أَدُلُّكُمْ عَلَى شَيْءٍ إِذَا فَعَلْتُمُوهُ تَحَابَبْتُمْ أَفْشُوا السَّلَامَ بَيْنَكُمْ ». رواه مسلم

***Kulongosola:***

***Hadith yi ikutilimbikitsa pa chinthu chofunikira zedi, dziwani kuti ndiko kukondana wina ndi nzake. Mneneri SAW akutiuza kuti ndithu ifeyo sitingakalowe ku jannat (ku munda wa mtendere) pokhapokha titakhulupirira mwa Allah ndipo sitingakhale okhulupirira oonadi mpaka titakondana wina ndi nzake. Ndipo kuti tikhale okondana pakati pathu pali kanthu kopepuka komwe tikakachita, chikondi chifala pakati pathu. Kanthu kopepukako ndiko kufalitsa salaam. Choncho kufalitsa salaam ndiko kuilengezetsa ndi kuipereka pakati pa anthu. Kuchokera mu hadith iyi tadziwa kuti ndithu kupereka salaam pakati pa Asilamu ndi njira yodzetsa chikondi pakati pawo. Ndipo kupeza chikondi ndi njira yoonjezera chikhulupiriro. Ndipo kuonjezera chikhulupiriro ndi njira yokalowera ku jannat (ku munda wa mtendere). Ndipo salaam yabwino m'mitundu ya salaam ndi kuyankhula munthu motere: " Assalaam alayikum warahmatullah wabarakaatuh". Pamene kuyankha kwa bwino koposa ndi: " Wa alayikum ssalaam warahmatullah wabarakaatuh". Koma ngati munthu atanena kuti " Assalaam alayikum warahmatullah", basi, kapena atanena kuti: " Assalaam alayikum " basi, kunena konseku n'kokwanira inshaa Allah.***

*Koma kunena mau onse oti: "(Assalaam alayikum warahmatullah wabarakaatuh" ) n'kwabwino zedi. Choncho Msilamu alimbikire kupereka salaam nthawi zonse ndipo asachite manyazi chifukwa kupereka salaam ndi njira yopezera malipiro, yoonjezera chikhulupiriro ndinso yolowera ku jannat (ku munda wamtendere).*

الحديث الثامنَ عشر

عَنْ أَبِي سَعِيدٍ الْخُدْرِيِّ رضي الله عنه قَالَ :
قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ « لاَ
يَنْظُرُ الرَّجُلُ إِلَى عَوْرَةِ الرَّجُلِ وَلاَ الْمَرْأَةُ إِلَى
عَوْرَةِ الْمَرْأَةِ » رواه مسلم

### Hadith 18

**Kuchokera kwa Abi Saeed Al-Khudriyy (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: " Munthu wa mwamuna asaone maliseche a mwamuna mnzake ngakhalenso munthu wamkazi asaone maliseche a mkazi mnzake". Muslim.**

***Kulongosola:***

***Hadith yi ikupereka lamulo lalikulu lofunikira kwambiri kwa ife kulidziwa ndi kuligwiritsira ntchito. Ndipo chimodzimodzi munthu wamawmuna kapena wamkazi ali ndi maliseche ndipo ayenera kuwabisa. Ndipo n'zoyenera kwa wina aliyense kuphimba maso kuti asaone malisechewo. Zimenezi ndi pakati pa munthu wa mwamuna ndi mwamuna mnzake ndiponso pakati pa munthu wamkazi ndi wamkazi mnzake kuli bwanji pakati pa wa mwamuna ndi mkazi ndinso wamkazi ndi wa mwamuna. Tikadziwa izi, tiyenera kusunga umaliseche wathu ndi kuwabisa kuti anthu asawaone. Ndipo tisanyalanyaze pa zimenezi mpang'ono pomwe, poleka kuwaona ngakhalenso kuwakhudza. Ndipo tiyenera kudziwa kuti pa chinthu ichi n'kosayenera kulekerera kapena kuchitira mphwayi angakhalenso kusereulira paliponse tingapezekepo.***

## Hadith 19

الحديث التاسعَ عشر

**Kuchokera kwa Al-Saab bin Jatha'mah (RA): Ndithu iye adampatsa Mtumiki wa Allah SAW mphatso ya nyama ya mtchire (yomwe adaipha) ndipo Mneneri SAW adaibweza kwa iye ndipo sadailandire. Ndipo pamene Mneneri SAW adaona kudandaula pa nkhope pake adati (kwa iye): " Ndithu ife sitidakubwezere (nyamai) pa chifukwa china ayi koma tili m'mapemhero a Hajj". Al-Bukhari ndi muslim.**

عَنِ الصَّعْبِ بْنِ جَثَّامَةَ ، أَنَّهُ أَهْدَى لِرَسُولِ اللّٰهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ صَيْدا ، فَرَدَّهُ عَلَيْهِ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ ، فَلَمَّا رَأَى رَسُولُ اللّٰهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ مَا فِي وَجْهِي ، قَالَ : إِنَّا لَمْ نَرُدَّهُ عَلَيْكَ إِلاَّ أَنَّا حُرُمٌ ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

*Nthawi zambiri ma sahaba (RA) adali kupereka mphatso kwa Mtumiki wa Allah SAW ndipo ndithu mwa chizolowezi adali kulandira mphatsozo ndi kupempherera zabwino. Pamene adali pa ulendo wa mapemphero a Hajj, adabwera kwa iye munthu dzina lake Al-Saab bin Jatha'mah (RA) atatenga nyama ya mtchire yomwe adaisaka kuti ampatse Mtumiki wa Allah SAW kuti adye ndipo Mneneri SAW sadalandire nyamayo chifukwa adali m'mapemphero a Hajj ndipo kupha nyama ya mtchire (pomwe muli m'mapemphero a Hajj kapena Um'rah) kuli mu gulu la zoletsedwa. Ndipo pamene adaibweza Mneneri SAW mphatso ya munthuyo, iye anadandaula (munthuyo) ndipo adaonetsa nkhope yodandaula ndi yokhumudwa, choncho mwamsanga Mneneri SAW adafotokoza chifukwa nati kwa iye: " Ndithu ife sitidakubwezere nyama pa chifukwa china ayi koma tili m'mapemphero a Hajj". Atamva izi Al-Saab bin Jatha'mah (RA) diso lake lidatonthola, ndipo adayamba kuphunzitsa anzake zimenezi naonso ophunzira ake adayamba kuphunzitsa anzao. Apa tikuphunzira kuti kufunikira kofotokoza chifukwa mwachangu pa chinthu chomwe mzako angachione molakwika, kuti asaganize zoipa ndi kuti satana asalowerere pakati panu. Uku ndi kugwiritsira*

*ntchito mawu a Allah wapamwamba adati: "Ndipo auze akapolo anga kuti (nthawi zonse) adzinena zomwe zili zabwino chifukwa satana amakhwirizira mikangano pakati pawo". Al-Isra 53.*

*Ndipo imam Al-Nnawawiyy adailemba hadith yi m'bukhu la Riyaadh Al- Ssaliheen pamutu oti 'Husnul-Khuluq' (Makhalidwe abwino) cholinga chofuna kutsindika ndi kufotokozera kuti ndithu kuluzanitsa maganizo ndi kuitonthoza mitima komanso kulongosola zifukwa zili mu gulu la makhalidwe abwino.*

## Hadith 20

**Kuchokera kwa Hudhaifah bin Al-Yamaan (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: " Sakalowa ku Jannah (ku munda wamtendere) kazitape ". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث العشرون

عَنْ حُذَيْفَةَ بن اليَمَانِ ، رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قال ، قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : « لاَ يَدْخُلُ الْجَنَّةَ قَتَّاتٌ ». متفق عليه.

*Kulongosola:*

*(Hadith iyi ikutichenjeza ife ku khalidwe lonyozeka ndipo ndi tchimo lalikulu lomwe likuwerengedwa mu machimo akuluakulu lomwe ndi ukazitape. Imeneyi ndi imodzi mwa mahadith amene akutichenjeza ku matenda a lilime ndipo alipo ambiri monga; miseche ndi ukazitape. Imam Al-Nnawawiyy (RA) adati: "Dziwa kuti ndithu zinthu ziwiri izi n'zoipitsitsa zedi ndipo ndi zomwe zafala pakati pa anthu kupatula ochepa okha). Ndipo mu hadith yi akutiletsa Mneneri wathu SAW khalidwe loipa lomwenso ndi tchimo lalikulu. Dziwani kuti khalidwe loipalo ndi ukazitape.*

*Liu loti: "Al-qattat" limatanthauza "Al-Namma'm" ndipo ku Chichewa likutanthauza kuti "Kazitape". Ndithu Mneneri SAW adatiuza kuti kazitape sakalowa ku jannah (ku munda wa mtendere). Liu loti "Al-Namiimah" limatanthauza kuti 'kutenga mau uku kupititsa uko ndi cholinga chodanitsa'. Iiyi ndi njira imodzi mwa njira zodzetsa mikangano, mavuto ndi udani pakati pa anthu. Choncho n'kofunika kwa Msilamu*

*aliyense wamwamuna ndi wamkazi kuti apewe ukazitape kupewa kwenikweni ndipo adzichenjeza ena ku ukazitapewo. Zili dero chifukwa ndi mchitidwe mwa machitidwe amene amamanitsa kukalowa ku jannah ndipo ndi chifukwa mwa zifukwa za mavuto a m'manda. Tikumpempha Allah atitchinjirize.*

## Hadith 21

**Kuchokera kwa Jabir bin Abdullah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Palibe Msilamu amene angabzale mbeu, ndipo munthu n'kumadyamo munthu kapena mbalame kapena chinyama (mbeuzo zitakhwima kapena zisanakhwime) pokhapokha (zimenezo) kwa iye imakhala sadaqah". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الحادي والعشرون

عَنْ جَابِرِ بْنِ عَبْدِ اللَّهِ رَضِىَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّه صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : « مَا مِنْ مُسْلِمٍ يَزْرَعُ زَرْعاً فَيَأْكُلُ مِنْهُ إِنْسَانٌ، أَوْ طَيْرٌ، أَوْ بَهِيمَةٌ إِلَّا كَانَ لَهُ بِهِ صَدَقَة ». متفق عليه

***Kulongosola:***

***Ulimi ndi ntchito yofunikira pa umoyo watsiku ndi tsiku. Ulimi umabweretsa chakudya ndi chuma. Ndipo mtendere wa Allah pa akapolo Ake ndi oti munthu akabzala mbeu iliyonse, munthu, mbalame kapena chinyama n'kudya, ndithu Allah amamulembera mlimiyo kuti wapereka sadaqah (chaulere) angakhale kuti pamene amabzala sadali ndi cholinga chopereka sadaqah koma amafuna chakudya kapena bizinesi. Izi si ulimi okha ai ngakhalenso ntchito iliyonse yabwino yomwe munthu akugwira ndipo wina n'kupindula nayo, amalipidwa. Monga yemwe wakumba chitsime namamwamo munthu kapena mbalame ngakhalenso chinyama kapena waika mthunzi penapake ndipo munthu nausapo kapena mbalame ngakhalenso chinyama, alinawo malipiro pa zimenezo. Izi zili deronso ku ntchito zabwino zina zonse zopindulitsa. Choyenera pochita izi munthu aikepo chiyembekezo choti alipidwa pamene akugwira ntchito zoterozo.***

## Hadith 22

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: "Mtumiki wa Allah SAW adali ndi ngongole ndi munthu wina wake (ndipo nthawi itakwana yolonjelera ngongole yake, munthuyo) adabwera kudzalonjelera ndipo adayankhula mopsa mtima (pa maso pa Mtumiki SAW), ndipo masahaba ataona izi zidawakhudza, nafuna kummenya munthuyo. Ndipo Mneneri SAW adati kwa iwo: "Musiyeni! Ndithu mwini chinthu ali ndi ufulu oyankhula."Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثاني والعشرون

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللهُ عَنْهُ قَالَ كَانَ لِرَجُلٍ عَلَى رَسُولِ اللهِ صلى الله عليه وسلم دَيْنٌ , أَتَى يَتَقَاضَاهُ فَأَغْلَظَ لَهُ فَهَمَّ بِهِ أَصْحَابُ النَّبِيِّ صلى الله عليه وسلم فَقَالَ النَّبِيُّ صلى الله عليه وسلم دَعُوهُ فَإِنَّ لِصَاحِبِ الْحَقِّ مَقَالًا ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Mneneri SAW adagula ngamila kwa munthu pa ngongole ndipo adagwirizana kuti adzam'patsa ndalama pa nthawi yakuti. Ndipo nthawi itakwana (yomwe adagwirizana) munthu uja adabwera kudzatenga ndalama kwa Mneneri SAW choncho adalowa kwa iye naitanitsa ndalama mokwiya ndi mokweza mau. Ndipo pamene masahaba (RA) adamva phokoso la mau ake adakwiya nayandikira kuti ammenye chifukwa sadaonetse khalidwe labwino pamaso pa Mtumiki wa Allah SAW. Apa Mneneri SAW adati kwa iwo: " Musiyeni ndithu mwini chinthu ali ndi ufulu oyankhula". Mu hadith yi tikupeza phindu lofunikira lomwe lingatithandize m'kachitidwe kathu ndi anthu. Ukutu ndiko kuti munthu akakhala akuitanitsa chinthu chake n'koyenera kwa ifeyo kuti timumvetsere komanso tiikire mtima pa mawu akewo. Ndikutinso tisamulange atati akweze mawu ake kapena wayankhula kena kake mopsa mtima. Ndithu titagwiritsira ntchito chikhalidwe cha Mnenerichi SAW pakati pathu, maufulu a anthu adzalemekezedwa mavuto pakati pathu adzachepa, mngwirizano udzakhazikika ndipo mikangano idzatha.***

## Hadith 23

**Kuchokera kwa Abi Qataadah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Amene akonde kuti Allah akamupulumutse ku mavuto a tsiku la Al-qiyaamah (loima pa maso pa Allah nthawi yaitali) apeputsire wosimidwa (popereka ina nthawi yobweza ngongole) kapena amukhulululukire (ngongole yake)". Muslim.**

**الحديث الثالث والعشرون**

**عَنْ أَبِي قَتَادَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ: قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صلى الله عليه وسلم « مَنْ سَرَّهُ أَنْ يُنْجِيَهُ اللَّهُ مِنْ كُرَبِ يَوْمِ الْقِيَامَةِ فَلْيُنَفِّسْ عَنْ مُعْسِرٍ أَوْ يَضَعْ عَنْهُ ». رواه مسلم**

***Kulongosola:***

***Tsiku la Al-Qiyaamah ndi tsiku lomwe Allah akaonetse anthu zomwe adachita aliyense payekha, akafunsa ndi kwalipira malipiro mofanana ndi ntchito zao zabwino kapena zoipa ndipo akagamula milandu yomwe idalipo pakati pao kenako akalamula ena ku jannat pomwe ena ku ng'anjo ya moto.***
***Patsikuli mavuto akachuluka kwa anthu chifukwa zochitika pa tsikuli n'zodabwitsa ndiponso n'zosasimbika. Choncho amene akufuna kuti Allah akamuombole ku zosasimbika ndi mavuto atsikuli ayenera amupeputsire wosimidwa pomupatsa nthawi yobweza ngongole kapena kupungule kapena kumukhulululukire kumene. Ndipo kupungula ngongole kwa wosimidwa kapena kukhululuka kumene ndi ntchito yabwino yotamandika ndipo ndi mustahabb (kuchita mwachifuniro) osati waajib (mokakamiza) ai. Liu loti 'Al-Tan fiis' ndiko kupereka danga lobweza ngongole kwa wosimidwa, pomwe 'Al-Wadha' ndi kupungula/kuchepetsa ngongole kwa wosimidwa kapena kukhululuka kumene. Choncho akatenga wina wake ngongole, nthawi yobweza n'kudutsa ndi kudziwa kuti ndithu iye (mnzakoyo) zamvuta kotero sangathe kubweza panthawiyo, basi mupatse nthawi ina kapena pungula, kapena khululuka potero udzapeza zabwino zochuluka ndipo pali chitsimikizo choti ukaomboledwa ku mavuto a tsiku la Al-Qiyaamah ndi chipambano cholowa ku jannat ndi kupeza chisangalalo cha Allah pa iwe.***

**Hadith 24**

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: "Mtumiki wa Allah SAW adati: "Yemwe watinyenga (watichita chinyengo) sali mwa ife". Muslim.**

الحديث الرابع والعشرون

عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللهُ عَنْهُ: قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صلى الله عليه وسلم: « مَنْ غَشَّنَا فَلَيْسَ مِنَّا ».

رواه مسلم.

***Kulongosola:***

***Nthawi zina Mneneri SAW adali kupita ku msika mmisika ya mu mzinda wa Madinah ngakhale tsiku logwa mvula. Ndipo tsiku lina akuyenda mu msika adadutsa pa munthu yemwe amagulitsa milu ya zakudya (monga tiligu ndi zina) ndipo zidali zitanyowa ndi mvula koma adabisa (zonyowazo) naika pansi pa muluwo kuti wogula asaone. Mneneri SAW adazindikira kuti ndithu mkati mwa katundu, muli cholakwika, choncho adalowetsa mkono wake m'chakudya chija napeza chinyontho. Atadziwa izi adamulangiza munthu uja nati kwa iye: "Koma bwanji ukadaika zonyowazi pamwamba kuti ogula adziona! " Yemwe watinyenga (watichita chinyengo) sali ndi ife".***

***Izitu zikutanthauza kuti wogulitsa malonda akhale wosabisa, wonena zoonadi wosachemerera malonda omwe ndi wosayenera ndipo asakweze mtengo mosayenera. Mu hadith yi muli kuletsa kuchita tchimo lonyasa ngati limeneli – chinyengo – ndipo muli kulimbikitsa anthu kuti atalikirane ndi m'chitidwe. Ndithudi chinyengo pa malonda, ntchito, malangizo, maphunziro ndi zina nzoletsedwa pa chipembedzo cha Allah.***

**Hadith 25**

**Kuchokera kwa Abi-Umaamat (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: " Yemwe watenga chinthu cha munthu Msilamu kudzera mu kulumbira kwake (konama), ndithu Allah wagamula za kumulowetsa iye ku moto ndipo jannah kwa iye ndi haram (yoletsedwa), Ndipo munthu wina wake adati: "O! Iwe Mtumiki wa Allah! Kodi angakhale kachinthu kochepa? Mtumiki SAW adati: "Ngakhale katakhala ka mtengo ka mswachi". Muslim.**

الحديث الخامس والعشرون

**عن أبي أُمَامَةَ رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: « مَنِ اقْتَطَعَ حَقَّ امْرِئٍ مُسْلِمٍ بِيَمِينِهِ، فَقَدْ أَوْجَبَ اللهُ لَهُ النَّارَ، وَحَرَّمَ عَلَيْهِ الْجَنَّةَ»، فقال رجل: يا رسولَ الله، وإن كان شيئاً يسيراً؟ قال: «وَإِنْ قَضِيباً مِنْ أَرَاك». رواه مسلم.**

***Kulongosola:***

***Mwa zinthu zina zomwe Chisilamu chidalimbikitsa kulimbikitsa kwenikweni ndiko kulemekeza maufulu a anthu. Choncho sikoyenera kwa ife kuphwanya ufulu potenga chinthu chake monga chuma ndi zina mwa upandu. Mu hadith yi Mneneri SAW akutichenjeza kutenga chinthu cha mwini ndipo akutiuza kuti ndithu yemwe atenge chinthu cha Msilamu kudzera mu kulumbira kwabodza, malipiro ake ndi kukalowetsedwa ku moto ndipo jannat kwa iye ndi haram yoletsedwa. Pamene masahaba adamva mau amenewa adafunsa iye nati: O! Mtumiki wa Allah SAW, "Kodi ngakhale (chotengedwacho) chitakhala chinthu chaching'ono? Zikutanthauza kuti chilango chachikulu chimenechi chilinso kwa yemwe atenge kanthu kochepa? Ndipo Mneneri SAW poyankha adati: " Ngakhale kandodo ka mswachi." Ndithu kutenga chuma cha anthu ndi kuphwanya ufulu wao ndi chinthu choipa zedi ngakhale chotengedwacho ndi chochepetsetsa ngati ka mtengo koswachira m'mano. Tim'pemphe Allah chikhululuko ndi umoyo wathanzi.***

### Hadith 26

**Kuchokera kwa Abi Musa Al- Ash'ariyy (RA) adati: "Ndithu Mneneri SAW adam'tuma iye pamodzi ndi Mu'az kupita ku Yemen ndipo adati kwa iwo awiriwo: "Fewetsani ndipo musakakitse, sangalatsani (ndi mau abwino) ndipo musathawitse (anthu), tsatirani ndipo musasiyane maganizo". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث السادس والعشرون

عن أبي موسى الأشعريِّ رضي الله عنه، أنَّ النبيَّ ﷺ بَعَثَهُ ومعاذاً إلى اليَمَن، وقال لهما: «يَسِّرَا وَلَا تُعَسِّرَا، وبَشِّرَا ولا تُنَفِّرَا، وَتَطَاوَعَا وَلَا تَخْتَلِفَا». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Mneneri SAW adatuma masahaba awiri olemekezeka kupita ku Yemen Abi Musa Al- Ash'ariyy (RA) ndi Mu'az bin Jabal (RA) Kukafalitsa chipembedzo ndi kuphunzitsa anthu. Ndipo asadapite awiriwa, Mneneri SAW adawalangiza ndi mau ochepa m'mayankhulidwe, akulu m'matanthauzo. Adati kwa iwo: Fewetsani ndipo musakakitse. Chitani ubwino ndi anthu, fikitsani chipembedzo kwa iwo mosakakitsa (mosakhwimitsa) khalani nao mololelana, ndipo auzeni kuti chipembedzo ndi chofewa, chilibe zosautsa, zochitika n'zosavuta. Adati kwa iwo: "Sangalatsani (ndi mau abwino) ndipo musathawitse". Kutanthauza kuti auzeni anthu zowasangalatsa zomwe zingadzetse chilakolako chopita nacho patsogolo osauza zinthu zomwe zingathawitse, kutsekereza ku chikhulupiriro ndi ntchito zabwino. Ndipo kenako adauzidwa mau achitatu ofunikira kwambiri kwa ena aliwonse awiri komanso a pachinzake kuti: Tsatirani ndipo musasiyane maganizo. Kutanthauza kumvana ndi kuchita chinthu limodzi ndipo ngati wina akuchita chinthu chabwino wina atsatire mnzake pa chimenecho kutero chikondi chidzakhazikika pakati panu ubwenzi wanu udzankerankera patsogolo. Kuchokera apa tikupeza phindu loti ndithu mnzako ndi amene atsatira mnzake mmene angathere ndipo sasemphana maganizo ndithu kutero watsatira Sunnat pomwe wochulukitsa kusagwirizana, mikangano ndi kusiyana maganizo ndithu m'kachitidwe ngati kameneka ali kutali ndi Sunnat ya Mneneri SAW.***

## Hadith 27

الحديث السابع والعشرون

**Kuchokera kwa Abi Musa Al- Ash'ariyy (RA) adati: "Mtumiki wa Allah SAW adati: "Amene wanyamula pa ife chida (chophera kapena kuopsezera) sali mwa ife". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

عن أبي موسى الأشعريِّ رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: «مَنْ حَمَلَ عَلَيْنَا السِّلَاحَ فَلَيْسَ مِنَّا». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Chitetezo (kusamenyana kapena kusaphana mwachisawawa pa dziko) ndi mtendere waukulu mwa mitendere ikuluikulu yochokera kwa Allah Wapamwamba ndipo ndi chofunikira zedi pa umoyo. Ndithu Allah adapereka chitetezo kwa akapolo Ake. Allah Wapamwamba akuti: "Choncho amupembedze Mbuye wa nyumba iyi (Al-Kaabah amene adachititsa kuti athe kuyenda maulendo awiriwo Yemwe amawadyetsa nthawi imene Arab anzawo ali m'njala) ndipo amawapatsa chitetezo pomwe anzawo ali ndi mantha". Quraish 3-4.***

***Chifukwa chofunikira kusunga bata ndi mtendere pa mudzi kapena pa dziko adachenjeza Mneneri SAW kunyamula chida kuti aopseze nacho anthu ndikuthira mantha m'mitima mwao ndikuwaopseza ndi nkhondo. Kusamvera atsogoleri, kusatsatira malangizo awo ndi kulekana ndi jamaat (gulu) kulinso m'guli la chiopsezo. Mmau ake SAW mu hadith yi oti: "Amene wanyamula pa ife chida (chophera kapena kuopsezera nacho) sali mwa ife". Ndi umboni wokwanira kuti wochita zimenezi sali mwa otsatira ake SAW ndipo kuti ndithu kutero ndi tchimo m'machimo akuluakulu.***

**Hadith 28**

**Kuchokera kwa Abdullah bin Mughaffal (RA) Adati: Ndithu Mtumiki wa Allah SAW adaletsa kugenda ndi timiyala tating'onoting'ono ndipo adati: "Ndithu timeneti sitingaphe nyama, komanso sitingagonjetse (nato) adani koma ndithu titha kuswa dzino ndi kuthudzula diso".**
**Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثامن والعشرون

عن عبد الله بن مُغَفَّلٍ رضي الله عنه، أنَّ رسول الله ﷺ نَهَى عن الخَذْفِ، وقال: «إنَّهَا لَا تَصِيدُ صَيْداً، وَلَا تَنْكَأُ عَدُوّاً، وَلَكِنَّهَا تَكْسِرُ السِّنَّ، وَتَفْقَأُ الْعَيْنَ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Nthawi zambiri Mtumiki wa Allah amafunitsitsa kuphunzitsa anthu zowapindulira ndipo adali kuwachenjeza ku mavuto pa chipembedzo ndinso pa dziko lino tero Allah adam'chemerera iye nati: " Ndithu wakudzerani Mtumiki wochokera mwa inu. Zikumudandaulitsa Iye zomwe zikuvutitsani, Iye ngoikira mtima pa inu pokufunirani zabwino, Ndipo pa okhulupirira ngodekha ndiponso ngwachisoni". Al-taubah 128. Ndipo Allah adachita ubwino potumiza iye Allah akuti: " Ndithudi Allah adawachitira ubwino (waukulu) Asilamu powatumizira Mtumiki wochokera mwa iwo yemwe akuwawerengera ma ayah ake (ndime zake) ndi kuwayeretsa ndi kuwaphunzitsa buku ndi (mau a) nzeru. Ndithudi kale adali mu kusokera koonekera".***

***Al- Imran 164. Mu hadith yi Mneneri SAW adaletsa chinthu chomwe kale Chisilamu chisanadze anthu adali kuchita ndicho Al-Hadhif (kugenda ndi timiyala tating'onoting'ono) ndipo adanena chifukwa choletsera kuti sitingaphe nyama, sitingagonjetse adani koma ndithu titha kuswa dzino ndi kuthudzula diso" Kuletsa uku ndi kwa aliyense wamkulu ndi wa mng'ono koma kwa wa mng'ono nkofunikira chifukwa ndi omwe amachita zimenezi choncho nkoyenera kuchenjeza, kulangiza ndi kudziwitsa.***

## Hadith 29

الحديث التاسع والعشرين

عن أنس بن مالك رضي الله عنه، قال: «خَدَمْتُ النَّبِيَّ ﷺ عَشْرَ سِنِينَ، فَمَا قَالَ لِي أُفٍّ قَطُّ». متفق عليه

**Kuchokera kwa Anas bin Malik (SAW) adati: "Ndidatumikira Mneneri SAW kwa zaka khumi, ndipo sadaneneko mkomwe kwa ine uffin (mau a m'nyonzo). Al-Bukhar ndi Muslim.**

***Kulongosola:***

***Pamene adasamuka Mneneri SAW kuchoka ku Makkah nafika ku Madina, amake wa Anas bin Malik (RA) adadza naye Anas (pa nthawiyi ali ndi zaka khumi) nati (kwa Iye): O! Mtumiki wa Allah SAW, "Uyu ndi mwana wanga (dzina lake ndi) Anas ndadza naye kwa iwe kuti azikutumikira". Ndipo Mneneri SAW adamulandira. Kuchokera tsiku limeneli, Anas (RA) adali wotumikira Mneneri SAW ndipo samasiyana naye kupatulo ma ulendo owerengeka. Mu hadith yi akutiuza Anas (RA) za makhalidwe a Mneneri SAW. Iye adamtumikira Mneneri SAW kwa zaka khumi ndipo ndithu pa nthawi yonseyi sadamuyankhule mkomwe mau a okalipa, omunena ndinso odzudzula angakhalenso mau onyoza. Izi zikusonyeza makhalidwe a bwino a Mneneri SAW pamaso pa ma sahaba ake, ana, (anyamata achisodzera) chimodzimodzinso a ntchito ndi akuluakulu a maudindo ao. Mu hadith yi tikupindula phindu lofunikira kwambiri lomwe ndi lamulo la kudekha ndi omwe ali pansi pathu, mwa antchito komanso otumikira kuti iwo ndi anthu monga ife, choncho ndi kofunikira kwa ife pa maso pawo kuwalemekeza, kuwathokoza ndi kuwapatsa zao.***

## Hadith 30

الحديث الثلاثون

عن أبي هريرة رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: « إِذَا قَامَ أَحَدُكُمْ مِنْ مَجْلِسٍ ثُمَّ رَجَعَ إِلَيْهِ، فَهُوَ أَحَقُّ بِهِ ». رواه مسلم.

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Ngati mmodzi mwa inu wachoka pa malo pomwe adakhala kenako nabwerera (nafuna kukhalanso pa malopo), iye ndi woyenera kukhala pa malopo". Muslim.**

***Kulongosola:***

***Chipembedzo chathu ndi chipembedzo chokwanira sichinasiye kakang'ono kapena chachikulu zomwe nzothandiza pa umoyo uno ndi womwe uli nkudza pokhapokha chidafotokoza mwatchutchutchu. Zina mwa zinthu zothandizazo ndi zomwe atiuza mu hadith yi zokhudza mwambo wa kukhala pa malo kapena pa khamu la wanthu. Mwambowu ukuti, munthu akakhala pa malo kapena pa mpando kenako ndi kuchoka ndipo kenako nafuna kubwerera pamalopo, iyeyo ndi woyenera kukhala pa malopo osati wina ai. Izinso sikukhudzana ndi malo ena alionse omwe khwimbi la anthu lasonkhana monga m'misikiti, malo ophunzirira, m'makalasi ndi malo ena. Munthu akakhala pa mpando kenako nkuchoka kwa ka nthawi kochepa kenako nkubwerera pamalo, iye ndi oyenera pa mpando koma ngati atachoka kwa nthawi yaitali monga yemwe wachoka pambuyo pa pemphero la Dhuhur nabwerera pambuyo pa Asr, kapena wachoka pambuyo pa Magharib nkubwerera mawa lake choncho sali woyenera kukhala pamalo pomwe adakhala. Ndithu zindikirani kuti mikangano yambiri makamaka pakati pa atsikana imachititika chifukwa cha malo. Kotero tikatsatira chiphunzitso cha shariya cha malo athu tikukhalapo chikondi chikadakhazikika ndipo mikangano ikadachepa.***

## *Hadith 31*

***Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Udindo wa Msilamu pa Msilamu (mnzake) ndi okwana usanu ndi umodzi (6): Ukakumana naye, pereka salaam, akakuitana, muyankhe, akakupempha langizo, mulangize, akayetsemula nanena Alhamdulillah (kuyamikidwa konse ndi kwa Allah), m'pemphere chisoni kwa Allah (ponena kuti: "(Yarhamukallah " ), akadwala, kamuzonde ndipo akamwalira mperekeze ku manda. Muslim.***

الحديث الحادي والثلاثون

عن أبي هريرةَ رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: « حَقُّ الْمُسْلِمِ عَلَى الْمُسْلِمِ سِتٌّ: إِذَا لَقِيتَهُ فَسَلِّمْ عَلَيْهِ، وَإِذَا دَعَاكَ فَأَجِبْهُ، وَإِذَا اسْتَنْصَحَكَ فَانْصَحْ لَهُ، وَإِذَا عَطَسَ فَحَمِدَ اللّٰهَ فَشَمِّتْهُ، وَإِذَا مَرِضَ فَعُدْهُ، وَإِذَا مَاتَ فَاتْبَعْه ». رواه مسلم.

*Kulongosola:*
*Zoyenera kuchita Msilamu kwa Msilamu mnzake zilipo zofunikira zambiri zina mwa izo ndi zisanu ndi chimodzi zatchulidwa mu hadith yi. Choyamba: Kupereka salaam. Pamene wakumana ndi mnzako mpatse salaam ndipo ngati iye wapereka salaam muyankhe. Chachiwiri: Kuyankha kuitana. Ngati wakuitana, pita kayankhe kuitanako makamaka ku phwando la nikaah ndithu kuyankha kuitanidwa ku phwando la nikaah ndi kofunikira ndi Waajib (kokakamiza).*

*Chachitatu: Kupereka langizo. Ngati mnzako wakupempha kupereka langizo kapena wakufunsa kena kake, mulangize mwachoonadi ndi moyera mtima.*

*Chachinai: Kupempha chisomo kwa Allah. Mnzako akayetsemula ndi kunena kuti*
*Alhamdulillah (kuyamikidwa ndi kwa Allah) nena kwa iye Yarhamukallah (Allah akuchitire chisoni) ndipo iweyo ngati wanena Yarhamukallah kwa mnzakoyo, naye abwezere ponena kuti Yahadiikumullah wayuswilihu baalakum (Allah akuongolereni ndinso akukonzereni zinthu zanu ndi chikhalidwe chanu). Chachisanu: Kumuzonda akadwala. Ngati Msilamu mnzako wadwala, kamuzonde. Dziwa kuti kuzonda wodwala kuli ndi ubwino waukulu ndi malipiro abwino kwa Allah.*

*Chachisanu ndi chimodzi: Kuperekeza janaaza mpaka kumanda (kwa amuna okha). Zofunikira Msilamu kwa Msilamu mnzake ndi zopitirira ngakhale atamwalira monga kum'perekeza ku manda choncho pitani mukam'pempherere, kenako m'perekezeni kumanda kokamuika. Kuteroku nkwabwino zedi kwa iye wakufa chifukwa mum'pemphera dua ndi kwa inu amoyo chifukwa mupeza malipiro.*

## Hadith 32

**Kuchokera kwa Abi Sa'id Al-Khuduriy (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Chitani zoyenera pa mseu". Iwo adati: "Ndi ziti kwa ife zoyenera za pa msewu"? Adayankha nati: "Kutsitsa maso (kusayang'anitsitsa zoletsedwa), kusavutitsa (anthu oyenda), kuyankha salaam, kulamula za bwino ndi kuletsa zoipa". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثاني والثلاثون

**عن أبي سعيد الخدري** رضي الله عنه، **قال: قال رسول الله ﷺ: «أَعْطُوا الطَّرِيقَ حَقَّهُ»، قالوا: وما حقُّه؟ قال: « غَضُّ الْبَصَرِ، وَكَفُّ الْأَذَى، وَرَدُّ السَّلَامِ، وَالْأَمْرُ بِالْمَعْرُوفِ وَالنَّهْيُ عَنِ الْمُنْكَرِ».** متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Nthawi ya Mneneri SAW anthu adali kukhala m'mphepete mwa msewu. Adali kusonkhana, kukambirana ndi kucheza. Ndipo Mneneri SAW adati kwa iwo: "Musakhale m'mphepete mwa msewu". Iwo Adati kwa iye: O! Mtumiki wa Allah SAW! Ndithu palibe kuchitira mwina pokhapokha kukhala mu msewu. Ndipo SAW adati:" (Choncho) chitani zoyenera za pa msewu". Iwo adati: "Ndi ziti kwa ife zoyenera za pa msewu"? Ndipo iye SAW adawauza zinthu zinayi.***

***Choyamba: Kutsitsa maso. Yemwe wakhala m'mphepete mwa msewu, naona nyumba yotsegula, sayenera kuyang'anitsitsa. Chimodzimodzi ngati waona mkazi, ayenera kutsitsa maso ake chifukwa Allah akuti: "Auze Asilamu achimuna kuti azyolitse maso awo." An-nur 30.***

***Chachiwiri: Kusavutitsa anthu oyenda powatchingira, ndipo osatailamo zinyalala ndi zonyasa ndi zina zotere.***

***Chachitatu: Kuyankha salaam. Ngati wina atapereka salaam ndi zoyenera kwa okhala m'mpepete mwa msewu kuyankha salaam. Kupereka salaam ndi sunnat pomwe kuyankha ndi waajib (kokakamiza). Allah akunena: "Ndipo pamene mwalonjeredwa kulonjeredwa kwa mtundu uliwonse (salaam) vomerani***

*(yankhani) ndi malonje abwino oposa amenewo kapena bwezani ofanana nawo". An-Nisa 86.*
*Chachinayi: Kulamula zabwino ndi kuletsa zoipa. Allah awatamanda anthu okhulupirira ndi matamando ndithu chifukwa cholamula zabwino ndi kuletsa zoipa. Allah Wapamwamba akuti: "Okhulupirira aamuna ndi okhulupirira aakazi ndi abwenzi omvana pakati pawo. Amalamula zabwino ndi kuletsa zoipa ndipo amapemphera Swalaat ndi kupereka chopereka (Zakaat). Ndipo amamvera Allah ndi Mtumiki wake. Awo ndi omwe Allah adzawachitira chifundo. Ndithu Allah Ngwamphamvu zoposa Ngwanzeru zakuya". At-Taubah 71.*

## Hadith 33

**Kuchokera kwa Abdullah bin Umar (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Sikoloredwa kwa munthu Msilamu yemwe ali ndi kanthu koti asiye chilawe (will - chikalata chosonyeza maina a anthu oyenera kudzalandira chuma cha masiye) ndi kugona masiku awiri asanalembe (wiloyo) koma kuti wilo yakeyo ikhale kwa iye yolembedwa (yokonzedwa)". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثالث والثلاثون

**عن عبد الله بن عُمَرَ رضي الله عنه، قال: قال رسول الله صلى الله عليه وسلم: «مَا حَقُّ امْرِئٍ مُسْلِمٍ لَهُ شَيْءٌ يُوصِي بِهِ، يَبِيتُ لَيْلَتَيْنِ إِلَّا وَوَصِيَّتُهُ مَكْتُوبَةٌ عِنْدَه». متفق عليه.**

*Kulongosola:*

*Hadith yi ndi umboni kuti kulemba chilawe ndi lamulo kwa iye amene ali ndi kanthu kosiya kuti osiyidwa adzalandire. Ngati munthu ali ndi ngongole kapena ndi woyenera kupereka Zakaat koma sadapereke kapena adasungitsidwa katundu ndi zina zotere ndipo sadabweze kwa mwini, kulemba chilawe kwa iye ndi waajib n'kokakamiza). Ndipo kwa ena osati uyu kulemba chilawe ndi sunnat monga kulemba kuti wakuti adzalandira chigawo chimodzi mu zigawo zitatu cha chuma (kapena kucheperako) m'ma polojekiti a za chifundo ndi zabwino. Zina zabwino tingakumbutsane ndi zakuti ndithu chilawe chilibe kuti ichi chuma*

*a n'chochepa koma ndithu wopereka chilawe alembe mooneka, momveka bwino pa chipepala kapena pa email (imelo) kapena pa ma uthenga apa foni kapena kuyankhula basi, zonsezi ndi njira zovomerezeka komanso zabwino inshaa Allah.*

## Hadith 34

**Kuchokera kwa Abdullah bin Umar (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adati: "Ndithu Allah wakuletsani inu kulumbirira abambo anu ndipo amene akhale akulumbira ndiye kuti alumbirire m'dzina la Allah kapena akhale chete". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الرابع والثلاثون

عن عبد الله بن عُمَرَ رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: «إِنَّ اللهَ يَنْهَاكُمْ أَنْ تَحْلِفُوا بِآبَائِكُمْ، مَنْ كَانَ حَالِفاً فَلْيَحْلِفْ بِاللهِ أَوْ لِيَصْمُتْ». متّفقٌ عليه.

***Kulongosola:***

*Masahaba atangolowa Chisilamu adali kulumbirira m'dzina losati la Allah potengera nthawi ya mdima iwo asadalowe Chisilamu monga kulumbirira abambo awo, amai awo, ulemerero ndi kukhulupirika ndi zina zotere.*

*Choncho mneneri SAW adaletsa ndipo Umar bin Al-Khatab (RA) adali mmodzi mwa amene adamva chiletso ndipo popanda kuzengereza adatsatira. Kuyambira pompo sipadadutse pa lilime lake kulumbirira kwina posakhala m'dzina la Allah nthawi zonse. Atalandira hadith yi Abdullah bin Umar adati: Umar (RA) adati: "Choncho Wallah (ndilumbirira Allah) sindidalumbirireponso nditamva chiletso kuchokera kwa Mneneri SAW. Ndipo izi ndi zomwe zili waajib kwa Msilamu kutsatira motsimikiza osati mopeneka kapena mwapendapenda.*

*Zina mwa zitsanzo pa nthawi ino zolumbirira monga kulumbirira ponena kuti "wahayaatika" (ndilumbirira umoyo wako), kapena "wannabiy " (ndilumbirira Mneneri) kapena "wal- kaabat " (ndikulumbirira kaabat).*

*Kulumbirira konga uku ndi haram (koletsedwa) ndipo ndi shirk (kuphatikiza Allah ndi zina). (Tsiku lina) Abdullah bin Umar (RA) adamva munthu akulumbirira adati "Wal- kaabat " (ndikulumbirira kaabat) ndipo Ibin Umar (RA) adati: "Usalumbirire (zina) posakhala Allah, ndithu ine ndidamva Mtumiki wa Allah SAW akunena kuti: "Amene walumbirira (wina) osati Allah ndithu (kafara) wakanira kapena (ash'raka) waphatikiza Allah ndi zina. Adailandira ndi Ahmad, Abu Daud ndi Tirmidhiy ndipo Tirmidhiy adati: "Iyi ndi hadith hassan (yabwino). Ndipo Al-shykh Al-Baaniy (rahmahullah) adaiika m'gulu la Sahih.*

### Hadith 35

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: "Sadachinyazitseko Mneneri SAW chakudya, ngati wachikhumba amadya, apo ayi amachisiya (osadya)". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الخامس والثلاثون

عن أبي هريرةَ رضي الله عنه قال: «مَا عَابَ النَّبِيُّ ﷺ طَعَاماً قَطُّ، إِنِ اشْتَهَاهُ أَكَلَهُ، وَإِلَّا تَرَكَهُ». متفق عليه.

*Kulongosola:*

*Ndithu Mneneri SAW adali ndi makhalidwe abwino, amakonda kuyankhula mau abwino ndipo amadana ndi mau oipa. Mu hadith yi muli khalidwe mwa makhalidwe a Mneneri SAW. Iye SAW sankanena mau ena alionse kupatula abwino. Zina mwa izo ndi zakuti Iye SAW ankati akapatsidwa chakudya ndithu samachipezera chifukwa monga kunena koti chakudyachi chozizira, choipa, chosapsa, sichabwino, kapena kunena kuti chakudyachi ndi chochepa, mchere sudakwane ndi ena mau amnyozo ngati otere. Ndithu iye SAW china mwa chizolowezi chake ankati akachifuna chakudya amadya ndipo ngati sadasangalatsidwe nacho, amachisiya osachinyoza. Ndithu ndi kofunika kwa ife kutsatira chitsanzo cha Mneneri SAW kotero tisachinyazitse chakudya kapena kuchfunira zifukwa koma nthawi zonse tizithokoza Allah pa mtendere omwe akutiptsa. Tisanene kenakalikonse pokhapokha mau abwino komanso tisayankhule mawu amtundu wina wake kupatula abwino.*

## Hadith 36

الحديث السادس والثلاثون

**Kuchokera kwa Al-barra'i bin A'zib (RA) adati: Mtumiki wa Allah SAW adali wokongola nkhope kuposa anthu onse, wabwino kuposa iwo m'kalengedwe, sadali wamtali moonekera ndiponso sadali wamfupi. Al-Bukhariy ndi Muslim.**

عن البراء بن عازبٍ رضي الله عنه، قال: «كَانَ رَسُولُ اللهِ ﷺ أَحْسَنَ النَّاسِ وَجْهاً، وَأَحْسَنَهُمْ خَلْقًا، لَيْسَ بِالطَّوِيلِ الْبَائِنِ، وَلَا بِالْقَصِيرِ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Adali Mneneri SAW wa chikhalidwe chabwino kuposa onse choncho Allah akunena za iye kuti: " Ndipo ndithu uli nawo makhalidwe abwino kwambiri ". Al-qalam 4. Ngakhale adali ndi chibadwidwe chokongola adalinso ndi makhalidwe abwino. Pa ichi, Swahaba wotchedwa Al-barra'i bin A'zib (RA) adati: "Adali Mtumiki wa Allah SAW wokongola nkhope mwa anthu onse, wabwino makhalidwe ndi kalengedwe. Sadali wamtali moonekera ndiponso sadali wamfupi koma adali wapakatikati. Mu hadith ina Al-barra'i bin A'zib (RA) adati: "Adali SAW wa msinkhu wapakatikati, wotayana mapewa, watsitsi lomwe limafika ku msonga ya khutu, Ndidamuona atavala chovala chokhuthala cha mandalazi (mizere yake idali yofiira), sindidaonepo wokongola kuposa iye.***

***Ndipo Al-Bukhariy ndi Muslim (RA) adalandira kuchokera kwa Anas bin Malik (RA) ndithu iye adati: "(Adali Mtumiki wa Allah SAW azhara llaun) oyera kuyera kosakanikirana ndi kufiira. Abu Hurairah (RA) adati: "Adali Mtumiki wa Allah SAW woyera ngati (kuyera kopangidwa kuchokera ku) siliva. Ja'bir bin Samurah (RA) adati: Ndidamuona Mtumiki wa Allah SAW usiku, mwenzi utawala kwambiri, ndipo ndidayamba kumuyang'ana iye kenako (kuyang'ana) mwezi ndithu iye malinga ndikuona kwa ine adali wokongola kuposa mwenzi. Allah apereke mtendere ndi madalitso pa iye, akubanja ake ndi masahabah ake madalitso ochuluka.***

## Hadith 37

**Kuchokera kwa Amru bin Al-A's (RA) adati: "Ndidam'funsa Mneneri SAW: Ndi ndani mwa anthu ali wokondedwetsetsa kwa iwe"? Adayankha nati: "Aisha". Ndipo ndidati: "Nanga kwa amuna"? Iye adati: "Bambo ake". Kenako ndidati: Kenako ndi ndani? Iye adati: "Umar". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث السابع والثلاثون

عن عمرو بن العاص رضي الله عنهما، قال: سألتُ النبيَّ ﷺ: أيُّ الناس أَحَبُّ إليك؟ قال: «عَائِشَةُ»، قلتُ: مِنَ الرجال؟ قال: «أَبُوهَا»، قلت: ثُمَّ مَنْ؟ قال: «ثُمَّ عُمَرُ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Sahabah wolemekezeka Amru bin Al-A's (RA) ndi mmodzi mwa akuluakulu, wotchuka mwa masahabah a Mneneri SAW akutifotokozera ifeyo kuti iyeyo adam'funsa Mneneri SAW za yemwe ali wokondedwa kwa iye mwa anthu onse. Ndipo adamuyankha nati: "Aisha" mkazi wake. Kenako Amru (RA) adafunsa: "Nanga mwa amuna"? Iye adati: "Bambo ake" Abu-Bakar Al-Sidiq (RA). Kenako Amru adati: "Kenako ndani O! iwe Mtumiki wa Allah SAW?" Ndipo Mneneri SAW adati: "Umar bin Al-Khatab". Uku ndi kusankhika kwakukulu kwa masahaba atatuwa Aisha, Abubakar ndi Umar (RA) kuti iwowa ndi anthu okondedwetsetsa kwa Mneneri SAW. Zofunikira kudziwa ndi zakuti ndithu Ahal-sunnat wal-jamaat (Otsatira Qur'an ndi hadith ndinso ma sahabah ndi ena odziwika) amakhulupirira kuti ndithu masahabah anayi (atchulidwa pa mwambapa) ndi olemekezeka ndipo ulemelero wao uli monga alili pa ndondomeko ya udindo wa khalifa unayendera, Abubakar Al-sidiq kenako Umar bin Al-Khatab, kenako Uthman bin Affan kenako Alie bin Abi-Talib (RA). Amenewa ndi masahabah olemekezeka mu ummat (gulu) onse wa Muhmmad SAW. Ndipo ndikoyenera kwa ife kuwakonda, kuwalemekeza, ndikuwapemphera chisangalalo cha Allah pa iwo, Allah asangalale nawo.***

## Hadith 38

**Kuchokera kwa Anas bin Malik (RA) adati: "Ambiri mwa madua amene Mneneri SAW adali kupanga mobwerezabwereza " O! Mbuye wathu! Tipatseni zabwino pa dziko lapansi ndipo pa tsiku lomaliza mudzatipatsenso zabwino, ndi kutitchinjiriza ku chilango cha moto!". Al-Bukhariy ndi Muslim.**

الحديث الثامن والثلاثون

عن أنس بن مالكٍ رضي الله عنه، قال: كان أكثر دعوةٍ يدعو بها النبيُّ ﷺ: «اللَّهُمَّ آتِنَا فِي الدُّنْيَا حَسَنَةً وَفِي الْآخِرَةِ حَسَنَةً، وَقِنَا عَذَابَ النَّارِ». متفق عليه.

***Kulongosola:***

***Dua ndi ntchito mwa zintchito zabwino ndipo dua ndi chisonyezo chomukuza Allah ndi uyekhayekha Wake ndipo ndi njira yodzetsa chisomo, chikhululuko, chisangalalo, chikondi ndi kulandiridwa ndi kupatsidwa zabwino Zake. Ndithu Mneneri SAW adali kuchulutsa ma dua. Madua amene afala mmabuku ambiri a sunnat ena mwa iwo ndi Sahih Al-Bukhariy, Sahih Muslim, Sunan Abi-Daud, Sunan Al-trimidhiy, Sunan Al-nasa'iy ndi Sunan Ibn Ma'jah amenewo ndi maduwa ake SAW. Ngakhale kuti madua a Mneneri SAW ndi ambiri koma Iye SAW adali kubwerezabwereza dua iyi " O! Mbuye wathu! Tipatseni zabwino pa dziko lapansi ndipo pa tsiku lomaliza mudzatipatsenso zabwino, ndi kutitchinjiriza ku chilango cha moto!" Zili dero chifukwa duayi ndi yaikulu idalandiridwa mu Qur'an ndipo ikusonkhanitsa zabwino za dziko lapansi ndi tsiku lili nkudza.***

***Al-shykh Abdul-Rahman Al-Saadiyy adati: "Zabwino zimene zikupemphedwa pa dziko lapansi zitanthauza zonse zabwino zimene munthu amakhumba atazipeza monga riziq (chakudya) yabwino, kupeza mkazi/mwamuna wabwino, mwana wosangalatsa, mpumulo ndi mtendere, maphunziro abwino, ntchito yabwino ndi zina. Zabwino za tsiku lili nkudza monga kupulumuka ku mavuto a m'manda, tsiku loima pa maso pa Allah, moto, kupeza chisangalalo cha Allah, chipambano cha mtendere okhazikika, ndi kuyandikira kwa Mbuye, Wachisoni".***

***Choncho dua yi idasanduka chiomba mkota ndipo ndi yofunika kumaitsogoza. Ichi n'chifukwa chake Mneneri SAW adali kuchulutsa kunena dua yi ndipo amalimbikitsa ena kutero.***

### Hadith 39

**Kuchokera kwa Abi Hurairah (RA) adati: "Mtumiki wa Allah SAW adati: "Munthu akamwalira, ntchito zake (zopezera malipiro kwa Allah) zimathera pompo kupatula zitatu: Sadaqa yoyenderera kapena maphunziro akuthandizidwa nawo (anthu ena) kapena mwana wabwino akumupangira dua". Muslim**

الحديث التاسع والثلاثون

عن أبي هريرة رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: « إِذَا مَاتَ الْإِنْسَانُ انْقَطَعَ عَنْهُ عَمَلُهُ إِلَّا مِنْ ثَلَاثَةٍ: صَدَقَةٍ جَارِيَةٍ، أَوْ عِلْمٍ يُنْتَفَعُ بِهِ، أَوْ وَلَدٍ صَالِحٍ يَدْعُو لَهُ ». رواه مسلم.

***Kulongosola:***

***Allah walamula akapolo Ake okhulupirira kugwira ntchito yabwino yowayandikitsa ku chisomo Chake, ndi kuwaombola ku mkwiyo ndi chilango Chake. Ndithu Mneneri SAW mu hadith yi watiuza kuti ndithu munthu akamwalira, ntchito yake yopezera malipiro kwa Allah imaduka kupatula ntchito zitatu zomwe ngakhale wamwalira koma amalipidwabe:***

***Yoyamba: Ngati adapereka sadaqa yopitirira asadamwalire monga kukumba chitsime, ndipo chitsimeko mkumagwira ntchito pambuyo pa imfa yake. Wina aliyense yemwe akupeza phindu pa chitsimecho, malipiro amapitabe kwa mwiniyo ngakhale ali mmanda. Chitsanzo china kumanga misikiti, zipatala, ma madarasa, kugawa ma Qur'an ndi zina. Yachiwiri: Maphunziro amene anthu akupindula nawo. Amene aphunzitse anthu kapena awalalikire kapena alembe bukhu kapena athandizire kusindikiza bukhulo kapena kugawa nawo kapena kufalitsa kwa anthu ndithu malipiro ake ndi oyenderera ali ndi moyo ngakhalenso atamwalira.***

*Yachitatu: Mwana wabwino wammuna kapena wamkazi. Ngati munthu wamwamuna kapena wamkazi wasamalira ana ake achimuna ndi achikazi kuwasamalira kwabwino, ntchito zao za bwino zomwe angagwire, malipiro ena amapita kwa bambo ndi mai omwe adawalera ndi kuwasamalira. Chimodzimodzinso mwana wa bwino amawapempherera makolo ake zabwino ndipo malipiro amapitabe kwa iwo. Makolo akapeza mtendere kwa Allah chifukwa chosamalira ana awo.*

## Hadith 40

**Kuchokera kwa Ja'bir bin Abdullah (RA) adati: "Mtumiki wa Allah SAW adati: "Adzadzutsidwa kapolo aliyense (kuchokera m'manda) ndi ntchito (yotsiriza imene pa nthawi ya imfa yake) adali kugwira". Muslim.**

الحديث الأربعون

عن جابر بن عبد الله رضي الله عنه، قال: قال رسول الله ﷺ: « يُبْعَثُ كُلُّ عَبْدٍ عَلَى مَا مَاتَ عَلَيْهِ ». رواه مسلم.

***Kulongosola:***

***Hadith yi ikukamba za mapeto abwino ndiyo ntchito yaikulu yomwe anthu ofuna zabwino adali kukangalika nayo kuyambira masahabah (RA) mpaka lero lino. Mapeto abwino ndiyo ntchito ya bwino imene munthu watsirizira kugwira pa umoyo wake monga chikhulupiriro ndi ntchito zina za bwino.***

***Mu hadith yi Mneneri wathu SAW akutiuza kuti ngati munthu wamwalira akuchita ntchito ina yake, ndithu adzadzutsidwa m'manda ndi ntchito imeneyo. Monga amene angamwalire uku ali m'mapemphero a Hajj akunena "Labbaika Allahumma labbaika", kapena ali m'mapemphero a Umrah ndithu adzadzutsidwa akutero. Ndipo amene amwalire akum'kumbukira Allah (zikir), adzadzutsidwa m'manda akum'kumbukira Allah, amene amwalire akuchita za utchimo adzadzutsidwa akuchita tchimolo. Timpemphe Allah chipulumutso ndi moyo wachikhulupiriro.***

*Choncho ndikofunikira kwa ife kutalikirana ndi ntchito zoipa ndipo nthawi yathu tiigwiritse ntchito podzadzitsa zinthu zabwino kuti titsirize umoyo wathu ndi zabwino ndipo potero kuti tidzadzutsidwe m'manda tili m'chisomo cha Allah, m'mchikhululuko ndi m'chisangalalo Chake.*

*Mau 0tsiriza*

***Ndikuyamika Allah, ndikum'thokoza Iye, ndikutchula mbiri Zake zonse zabwino, ndikupempha chikhululuko Chake, ndipo chisomo ndi chisangalalo zikhale pa ine ndi amene wawerenga mau anga. Kenako ndithu ine ndafuna kukudziwitsani za bukhuli motere:***

***1- Bukhu ili ndi loyenera aliyense wamkulu ngakhalenso wachichepere chifukwa mkatimu muli ndime za m'Qur'an ndi Hadith (mau, zochita ndi zovomereza za Mneneri SAW) ndinso malangizo kuchokera m'mabuku a anthu ozama pa maphunziro potenga mau ao kapena tanthauzo lake.***

***2- Ndidasankha Mahadith (afupiafupi) ndi cholinga choti (owerenga) aloweze pa mtima mosavuta ndipo ndasiyanitsa mitu ya Mahadith pofuna kuchulukitsa phindu kuchokera m'menemo.***

***3- Ndawaika Mahadith okwanirira motsogozana kumapeto kwa bukuli kuti akhale ofewa powasunga pa mtima ndi kuwawerenga***

***4- Ndasonkhanitsa Mahadith m'buku lotchedwa Ar-Baiina Al-Wil'daniyyah cholinga changa poyambirira chidali choti anyamata ndi atsikana achichepere aloweze pa mtima. Pa chifukwa chimenechi ndikulangiza za kukhazikitsa mipikisano ndi mapulogalamu oloweza Mahadith wa m'nyumba zao, mma madirasa mwao, m'makalasi ndi m'malo ena ophunzitsira.***

***5- Ndikuwalimbikitsa abambo ndi amai, aphunzitsi aamuna ndi aakazi kuti awawerengere ana ao bukuli koyamba asanayambe kuloweza pa mtima kuti lilime lao liongoke ndi kutinso aphunzitsidwe miyambo ya Chisilamu yoyenera yomwe tikupindula kuchokera m'Mahadith amenewa.***

***6- Ngakhale kuti ndayesetsa kulongosola matanthauzo a hadith, phindu lake kudzanso malangizo ake koma matanthauzo a Hadith ngochuluka choncho ndikufunitsitsa anyamata ndi atsikana atsirize pa okha kwatsalako ndipo adzipezere matanthauzo mothandizidwa ndi ena ndipo adzilemba zomwe apezazo kuti apindule iwo ndi ena. Ndithu kudziwa ndi kupambana kuli kwa Allah. Ndipo mtendere ndi madalitso zikhale pa Mneneri wathu Muhmmad.***